# Buku la Mphunzitsi

## Nthawiyabaibulo
## Kalasi Lachitatu ndi Lachinayi

Maphunziro C1 - C6

www.besweb.com

## Bible Educational Services

Registered Charity UK (No 1186004)

**Cholinga cha Utumiki**
Kukonzera ena maphunziro a Baibulo kuti apereke choonadi cha Yesu ku m'bado otsatira pa dziko lonse lapansi.

**Masomphenya a Utumiki**
Kupereka ku m'bado wotsatira maphunziro okwanira, m'chiyankhulo chawo powalembera ndi kuwathandiza komanso kuthandiza anzathu ena onse odzipereka pa dziko lonse.

## ZOYENERA KUDZIWA

**Zomwe a Bible Educational Services amachita**
A Bible Educational Services (BES UK) amasindikiza maphunziro a "Nthawiyabaibulo", "Moyo Watsopano" ndi "Okolola" a m'Chingerezi komanso amathandiza a Postal Bible Schools ndi mabungwe ena amene amagwiritsa ntchito maphunziro a BES ku UK ndi ku mayiko a kutsidya la nyanja pokawachezera, kugwira nawo ntchito limodzi, kuwalangiza ndi kuwaphunzitsa. BES imagwiranso ntchito pamodzi ndi magulu ena amene akugwira ntchito yomasulira maphunzirowa m'ziyankhulo zawo, pomasulira, kusindikiza ndi kupereka maphunziro kwa anthu ena. Maphunzirowa amaperekedwa mwaulere kwa ophunzira onse.

Maphunziro a Nthawiyabaibulo anayamba kugwiritsidwa ntchito ku Kumpoto kwa Ireland zake 60 zapitazo. A Bible Educational Services ndi amene ali ndi udindo woyang'anira ntchito yosindikiza maphunzirowa m'Chingerezi ndi m'ziyankhulo zina zonse. Maphunziro a Nthawiyabaibulo amasindikizidwa mu A4 ndipo amathandiza ophunzira m'madera ena kuti masabata anayi aliwonse azitha kutumiza mayankho ku Postal Bible School Centre kuti akachonge. Posachedwapa, tikuyamika a bungwe la Every Home Crusade (Bungwe la Chitsistimutso) ku Belfast, anayamba kusindikiza maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi amene amatchedwa A5. Amenewa amagwiritsidwa ntchito m'matchalichi ndi m'sukulu makamaka ku mayiko akunja kuti akhale osavuta chifukwa kumeneko njira zotumizira ndi zovuta kwambiri.

Maphunziro a BES ndi apadera kwambiri chifukwa amatha kugwiritsidwa ntchito m'nyumba kapena pa gulu (tchalichi kapena sukulu), potsatira ndondomeko imene imalola ophunzira kuphunzira kwa zaka makumi awiri. Gulu lililonse lili ndi maphunziro asanu molingana ndi zaka zawo, Amene sanayambe sukulu (Kalasi 0), zaka 5-7 (Kalasi Yoyamba), zaka 8-10 (Kalasi Yachiwiri), zaka 11-13 (Kalasi Yachitatu), zaka 14-16 (Kalasi Yachinayi). Pali ndondomeko ya kaphunzitsidwe ya zaka zitatu ya gulu lililonse molingana ndi zaka zawo. (Onani peji 4.) Magulu angathe kusintha molingana ndi kuthekera kwawo. A Bibletime Resource amapereka mpata kwa ana kuphunzira Mawu a Mulungu ndi kutha kuzindikira kufunika kwa Uthenga Wabwino pa miyoyo.

Maphunziro akupezeka m'Chingerezi pa BES website – www.besweb.com kapena kuchokera kwa Mlembi Wamkulu. Amapezekanso pa website ya ziyankhulo zina. BES ali ndi zomwe analemba zothandiza amene akufuna kugwira nawo ntchitoyi, ndipo zimenezi zilinso pa website yawo.

## Keyala

**International and Northern Ireland Secretary (stockist of all English lessons)**
Mr S Balmer, BES Office (UK), 37a Belmore Street, Enniskillen, Northern Ireland. BT74 6AA
Phone: 00 44 286 632 2462
Email: sam@besweb.com

**UK Secretary – Editorial feedback**
Mr Stephen Gillham
Email: stephen.gillham@besweb.com

**Web address:** www.besweb.com
**Email address:** info@besweb.com

## BUKU LA MPHUNZITSI

Poyamba, maphunziro awa anakonzedwa ndi cholinga choti akhale otumizira anthu, koma lero maphunzirowa akugwiritsidwa ntchito kwambiri pamene njira zotumizira ndi zosadalirika. M'madera ena monga ku mipingo ya ku Afrika, India ndi mayiko ena kulibe njira zotumizira zodalirika. Chifukwa cha ichi, Buku la Mphunzitsi linakonzedwa kuti lithandize amene sangathe kulandira pa positi. Buku la Mphunzitsi m'buku lino ndi la Kalasi Lachitatu ndi Lachinayi.

Buku la Mphunzitsi lililonse lili ndi ndime zonse zimene zili m'maphunziro a Nthawiyabaibulo. Maphunziro a Nthawiyabaibulo ndi Buku la Mphunzitsi zinakonzedwa kuti zigwire ntchito sabata lililonse. Maphunziro a mwezi wa Epulo amafotokoza za Paska ndipo a mwezi wa Disembala za Khirisimasi.

Madera ena amagwiritsa ntchito maphunziro a pa mwezi otchedwa A4, amene ali ndi maphunziro anayi ndipo ena amagwiritsa ntchito maphunziro otchedwa A5 amene ali ndi maphunziro 24. Mphunzitsi kapena mtsogoleri akuyenera kupereka maphunziro a A4, ndipo sabata lililonse azilemba mayankho a phunzirolo m'tchalichi, ku sukulu kapena ku nyumba ndi kupereka mayankhowo sabata lotsatiralo. Kumapeto kwa mwezi, mphunzitsi kapena mtsogoleri adzilandira maphunzirowo ndi kukachonga, akatsiriza abwere nawo ndi kupereka kwa ophunzirawo.

Ngati ophunzira akugwiritsa ntchito buku, mphunzitsi atenge bukulo kumapeto kwa phunziro lililonse ndi kukachonga. Koma tikudziwa kuti madera ena izi ndi zosatheka. Ngati akuphunzira m'kalasi, ophunzira asinthane mabuku awo ndipo mphunzitsi kapena mtsogoleri awathandize kupeza mayankho ndipo ophunzirawo achongelane maphunziro awo. Kumapeto kwa bukuli kuli malo oyika marikisi amene wophunzira wapeza mwezi uliwonse ndiponso malo a ndemanga ya mtsogoleri ya momwe wophunzirayo akuchitira m'kalasi. Palinso satifiketi yomwe wophunzira ayenera kulandira yoonetsa marikisi ake a maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi.

Timakondwera pamene anthu akutifotokozera zomwe akukumana nazo pogwiritsa ntchito Buku la Mphunzitsi ndi mabuku a Nthawiyabaibulo ndipo tumizani ndemangazo kwa stephen.gillham@besweb.com.

## KUKONZEKERA KWA APHUNZITSI

Buku la Mphunzitsi si lotsekeka kuti mphunzitsi sangathenso kuyikapo zinthu zina zomwe akuziona kuti ndi zothandiza pophunzitsa. Nawa malangizo othandiza pogwiritsa ntchito Nthawiyabaibulo.

- **Kudziwa bwino nkhani** - Aphunzitsi akuyenera kudziwa bwino nkhani ya m'Baibulo komanso phunziro la Nthawiyabaibulo lomwe akugwiritsa ntchito. Nkhani ndi yakuti, mphunzitsi awerenge phunzirolo nthawi yophunzitsa isanakwane. Iye amvetse bwino ndondomeko ya phunziro lililonse kuti akonzekere bwino kuphunzitsako.
- **Kumvetsa phunziro lokaphunzitsa** - Poyamba pa ndondomeko ya phunziro lililonse pali mawu akuti, "Ife tikuphunzira kuti" motsatidwa ndi zolinga ziwiri zophunzirira zomwe mwina ana angamvetse ngati mphunzitsi atafotokoza, kenaka pali gawo lotsiriza phunziro la Nthawiyabaibulo. Cholinga chophunzirira ndi kufuna kudziwa nkhaniyo, pamene chachiwiri ndi cholimbikitsa ophunzira kuti aganizire zomwe aphunzirazo ndi kuzigwiritsa ntchito pa moyo wawo. Zolinga zimenezi zikugwirizana kwambiri ndi fundo/choonadi cha m'phunzirolo ndipo aphunzitsi akuyenera kugwiritsa ntchito zimenezi kuti adziwe momwe aphunzitsira ndi zomwe ana aphunzira.
- **Mawu oyamba** - Maphunziro onse akuyamba ndi mawu akuti, "kumene kuli ana" ali ndi zomwe akukumana nazo. Pali njira zambiri zomwe tapereka zothandiza ana kutenga mbali pa zokambirana nthawi ya maphunzirowo.
- **Kuphunzitsa** - Fundo zazikulu za phunziro tapereka. Tikuyembekezera kuti aphunzitsi sadzikhalanso akumaziwerenga pamene akuphunzitsa koma kuti akhala atadziwa bwino nkhani yonse ndipo adzitha kufotokoza nkhaniyo mochititsa chidwi. Mphunzitsi ayesetse kuti ana amvetse mitu ya maphunzirowo kuchokera pa nkhani yomwe akuphunzira ndiponso awathandize kumvetsetsa zoyenera kuchita kuchokera mu nkhaniyo. Pamene m'poyenera tayesetsa kufotokozera bwino monga nkhani chabe. Mawu amenewa tawalemba motere: ***ITALICS***.
- **Kuphunzira** - Nkhani iliyonse ili ndi Vesi Yoloweza. Malo ena muli Mavesi Oloweza awiri; taonjezera vesi ina yomwe tikuona kuti itha kukhala yothandiza kuti ana aphunzire mosavuta. Tikukhulupirira kuti ana adzaphunzira Mavesi Oloweza ndipo aziwakumbukira kotero kuti adzadziwa mavesi ambiri.

- **Kutsiriza** - Kwa amene akuphunzira m'kalasi, mphunzitsi ayenera kudziwa ngati ophunzira angathe kutsiriza ntchito yawo ndiponso za thandizo lomwe likufunika kuchokera kwa mphunzitsiyo. Kwa ophunzira ena padzafunika kuti mphunzitsi aziwerenga nkhaniyo, ophunzirawo n'kumatsatira kapena kumvera. Koma enanso adzatha kuwerenga okha nkhaniyo. M'njira zonse ziwiri, ndi kofunika kuwauza malangizo okhudzana ndi mafunso. Ngati Nthawiyabaibulo sikuchitikira m'kalasi, n'kofunika kuti aphunzitsi azipezeka kuti azithandiza kuyankha mafunso osati aziyankha ngati a m'kalasi wamba. Ophunzira ayenera kumasangalala, kulimbikitsidwa ndi kuyamikiridwa pamene kuphunzira.
- **Kukumbutsana** - Zomwe zingatheke chitani, khalani ndi nthawi ya mafunso, ya masewero ndi zina zambiri. Izi zidzathandiza kuphunzira ndi kukumbukira pamtima nkhaniyo.
- **Kuonetsa** - Nthawi zina, zinthu zoti muonetse zidzakhala zovuta kuzipeza koma ngati n'kotheka yesetsani kupeza zithunzi kapena zida zina zothandiza kuti ophunzira amvetse nkhaniyo. Zinthu zimene ophunzira akuziona zimathandiza kwambiri pofotokoza nkhani. Pamene n'zotheka, pezani zithunzi kuchokera ku www.freebibleimages.org (FBI) zomwe mungathe kulandira. Kumapeto kwa Buku la Mphunzitsi kuli zina zoonjezera momwe akufotokoza kwina kumene mungapeze zithunzi za nkhani za m'Baibulo mwaulere.
- Ngati mungapeze fotokope mutha kukulitsa zithunzizo, kukhala za kalala ndi kuzigwiritsa ntchito pophunzitsa.

## Nthawi ya Phunziro

- **Machitidwe.** M'buku la Mphunzitsi muli machitidwe a phunziro lililonse, koma mphunzitsi ali ndi ufulu nthawi ndi nthawi kusintha machitidwe ake.

    1. Mawu Oyamba ndi kufotokoza nkhani - mphindi 15
    2. Kuphunzitsa Vesi Yoloweza – mphindi 5 mpaka 10
    3. Kutsiriza kulemba - mphindi 20
    4. Mafunso ndi zochitika zina mpindi 5 mpaka 10.

Kumbukirani mawu ofunika awa:

"Ndiuzeni ndipo ndidzayiwala,
ndionetseni ndipo ndidzakumbukira,
loleni ndichite nawo ndipo ndidzamvetsetsa."

## Zophunzitsa Nthawiyabaibulo

| | KALASI 0 (sanayambe sukulu)<br>Kalasi Yoyamba (Zaka 5-7)<br>Kalasi Yachiwiri (Zaka 8-10) | Kalasi Yachitatu<br>(Zaka 11-13) | Kalasi Yachinayi<br>(Zaka 14+) |
|---|---|---|---|
| **MAPHUNZIRO A** | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Abrahamu<br>6. Abrahamu<br>7. Petro<br>8. Petro<br>9. Yakobo<br>10. Akhristu Oyambirira<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Pemphero<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe ndi Kugwa<br>2. Zochitika Zoyamba - Genesis<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Moyo wa Chikhristu<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| **MAPHUNZIRO B** | 1. Moyo Woyambirira wa Khristu<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Mafanizo<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Alembi a Uthenga Wabwino<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yakobo ndi Banja Lake<br>7. Yosefe<br>8. Machitidwe 2:42 - Zoyenera Kuchita<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Lamulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| **MAPHUNZIRO C** | 1. Danieli<br>2. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>3. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute ndi Samueli<br>6. Davide<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Yona<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>3. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Amene Mulungu Anawagwiritsa Ntchito - Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Zoyankhula za Yesu<br>3. Mphamvu za Ambuye<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Ena a mu Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |

## C1 – KALASI 3
**Phunziro Loyamba – Danieli**
**Mutu – Dziko lachilendo**

**Werengani:** *Danieli 1: 1-21*
**Vesi Yoloweza:** *Mateyu 6: 33*

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Mulungu amakhala akulamulira ngakhale mu nthawi imene zinthu zavuta.
2. Danieli anateteza chimene ankakhulupirira.

### MAWU OYAMBA

Pezani zithunzi ziwiri za zakudya, chimodzi cha chipatso chathanzi ndi ndiwo za masamba ndipo china chokhala ndi zakudya zabwino za phwando. Funsani ana kuti angakonde chithunzi chiti pa ziwirizi, nanga n'chifukwa chiyani.

### KUTSIRIZA

**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Mfumu Nebukadinezara anagonjetsa Yerusalemu ndipo anatenga ziwiya za m'Nyumba ya Mulungu pamodzi ndi anthu ena kupita ku Babulo. ***(1: 1-2)***
2. Asipenazi, mkulu wa nduna zake, anasankha anyamata ochangamuka, owoneka bwino ndi anzeru kuti awaphunzitse zaka zitatu kuti adzagwire ntchito ya mfumu. ***(1: 3-5)***
3. Danieli sanafune kudya chakudya chopatsa thanzi cha mfumu chifukwa chinaperekedwa ku mafano. ***(1: 8)***
4. Danieli anapempha kuti azidya ndiwo zamasamba ndi kumwa madzi kwa masiku khumi chabe. ***(1: 11-14)***
5. Potsiriza pa nthawi imeneyi Danieli ndi anzake anapezeka kuti anali athanzi kwambiri kuposa amene ankadya chakudya cha mfumu. ***(1: 15-16)***
6. Mulungu anapereka kwa Danieli ndi anzake aja chidziwitso ndi kuzindikira bwino mitundu yonse ya zolembedwa ndi za maphunziro. Danieli anapatsidwa mphatso ya kuthanthauzira masomphenya ndi maloto. ***(1: 17)***
7. Kulimbikira ntchito kwa Danieli ndi anzake aja kunaonekera ndipo mfumu inakondwera nawo. Iye anaona kuti iwo anali anzeru kwambiri kuposa amatsenga onse mu ufumu wake wonse. ***(1: 20)***

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Loyamba.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Dziko lachilendo.

### KUKUMBUTSANA

Kodi mungapereke malangizo otani kwa Mkhristu amene akuyamba maphunziro pa sukulu yatsopano kapena kulowa kalasi ina? Kodi iwo akufanana motani ndi Danieli ndi anzake aja ku Babulo?

### KHALANI MOYO UMENEWU

**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Tikapezeka pa malo atsopano, kodi timayima pa choonadi?
2. Kodi ndinu wokonzeka kutsatira Mulungu ndi njira zake m'malo motsatira ena amene angakuchotseni pamaso pa Mulungu?
3. Kodi tikuphunzira chiyani pa nkhaniyi za kufuna kwa kudya zinthu zopatsa thanzi?

## C1 – KALASI 4
**Phunziro Loyamba – Danieli**
**Mutu – Kutumikira Mulungu**

**Werengani:** *Danieli 1: 1-7; 2: 1-49*
**Vesi Yoloweza:** *Danieli 2: 28*

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Danieli ndi anzake anadalira Mulungu kuti adzawathandiza ndi kuwapatsa mayankho amene ankawafuna.
2. Mulungu amakhala akulamulira ngakhale pamene takumana ndi zovuta.

### MAWU OYAMBA

Funsani ana asankhe mu mtima nambala pakati pa 1 mpaka 20, ndipo ana ena atchule nambala imene iwo asankhayo. Fotokozani kuti ife sitingadziwe zimene ena akuganiza. Mu phunziro la lero, Mfumu Nebukadinezara ankayembekezera kuti amatsenga ake adziwa loto lake popanda kuwawuza.

### KUTSIRIZA

**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Mfumu Nebukadinezara anagonjetsa Yerusalemu ndipo anatenga ziwiya za m'Nyumba ya Mulungu pamodzi ndi anthu ena kupita ku Babulo. ***(1: 1-2)***
2. Asipenazi, mkulu wa nduna zake, anasankha anyamata ochangamuka, owoneka bwino ndi anzeru kuti akawaphunzitse kutumikira mfumu. ***(1: 3-5)***
3. Mfumu inavutika mu mtima chifukwa cha maloto ake. Iyo inalamula kuti anthu anzeru amuwuze malotowo ndi kumasulira. ***(2: 1-2)***
4. Mfumu inati ngati anthu anzeru samukumbutsa malotowo ndi kufotokoza tanthauzo lake, onse adzaphedwa. Zotsatira zake, moyo wa Danieli ndi anzake aja unali pa chiopsezo. ***(2: 13)***
5. Danieli atazindikira zomwe zinkachitika, iye pamodzi ndi anzake aja anapempha Mulungu kuti awathandize. ***(2: 18)***
6. Mulungu anawulula malotowo ndi tanthauzo lake kwa Danieli ndipo Danieli anatamanda Mulungu chifukwa chomupatsa tanthauzo la malotowo. ***(2: 19-23)***
7. Danieli atakumana ndi mfumu, iye anawuza mfumu kuti ndi Mulungu yekha amene angathe kufotokoza tanthauzo la malotowo. Ndipo iye anawuza mfumu tanthauzo la malotowo. (2: 27-45) Ndipo mfumu inapereka maudindo a ulamuliro kwa Danieli ndi anzake aja. ***(2: 48-49)***

*(Mwina sikoyenera kuti muyesetse kufotokoza malotowo ndi kupereka tanthauzo lake.)*

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Loyamba.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kutumukira Mulungu.

### KUKUMBUTSANA

Kodi Danieli ndi anzake aja anachita chiyani atakumana ndi vuto lofuna kudziwa maloto?
Kodi ife tikuyenera kuchita chiyani tikakumana ndi nyengo zovuta? Werengani ***Afilipi 4: 6-7.***

### KHALANI MOYO UMENEWU

**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
Nthawi zina timakumana ndi zinthu zimene timaziona kuti ndi zosatheka. Mulungu anatha kuthandiza Danieli ndi anzake. Kodi Mulungu angachitenso izi kwa ife? Werengani ***Luka 1: 37.***

| | C1 – KALASI 3<br>**Phunziro Lachiwiri – Anzake a Danieli**<br>**Mutu – Ng'anjo yamoto** | C1 – KALASI 4<br>**Phunziro Lachiwiri – Danieli**<br>**Mutu – Kukhala mbali ya Mulungu** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Danieli 2: 48-49; 3: 1-30***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Danieli 3: 17***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Ngati ndife Akhristu, tikuyenera kukhala ngati Danieli ndi anzake atatu; tizikhala okonzeka kukhala mbali ya Mulungu ngakhale titakumana ndi zovuta zotani.<br>2. Ngati Ambuye Yesu akhala woyamba m'moyo mwathu, Iye adzatisamalira m'moyo uno ndi kudzatipatsa mphotho m'tsogolo chifukwa cha kukhulupirika kwathu kwa Iye. | **Werengani:** ***Danieli 3: 1-30***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Daniel 3: 17***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Monga Sadrake, Mesake ndi Abedinego anadalira Mulungu kuti adzawapulumutsa, ifenso titumikire Mulungu mokhulupirika.<br>2. N'kofunika kukhala mbali imene ndi yolondola. |
| **MAWU OYAMBA** | Kumbutsani ana kuti mu dziko la Babulo, anthu ankapembedza mafano. Fano la phunziro lino ndi lopangidwa ndi golide. Kutalika kwake kunali mamita 27 ndi mulifupi mwake mamita atatu. Nebukadinezara analamula kuti anthu akamva kuyimba kwa nyimbo, onse agwade ndi kupembedza fanolo. Koma anyamata atatu a Chihebri, Sadrake, Mesake ndi Abedinego, anakana kupembedza fanolo chifukwa iwo ankapembedza Mulungu woona. | Kumbutsani ana kuti mu dziko la Babulo, anthu ankapembedza mafano. Fano la phunziro lino ndi lopangidwa ndi golide. Kutalika kwake kunali mamita 27 ndi mulifupi mwake mamita atatu. Nebukadinezara analamula kuti anthu akamva kuyimba kwa nyimbo, onse agwade ndi kupembedza fanolo. Koma anyamata atatu a Chihebri, Sadrake, Mesake ndi Abedinego, anakana kupembedza fanolo chifukwa iwo ankapembedza Mulungu woona. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Sadrake, Mesake ndi Abedinego anakana kupembedza fano limenelo. ***(3: 12)***<br>2. Nebukadinezara anakwiya nawo ndipo anaopseza kuti awaponya m'ng'anjo yamoto. ***(3: 15)***<br>3. Sadrake, Mesake ndi Abedinego anawuza Nebukadinezara kuti ngakhale atawaponya m'ng'anjo yamoto, Mulungu angathe kuwapulumutsa. ***(3: 17)***<br>4. Pamenepo Nebukadinezara analamulira kuti ng'anjo ayitenthetse kasanu ndi kawiri kuposa nthawi zonse ndipo awaponyemo anyamata atatu a Chihebri. Ng'anjo inatentha kwambiri motero kuti anthu amene anaponya anyamatawo anaphedwa ndi motowo. Koma pamene mfumu inayang'anamo, inadabwa kuona anthu anayi – m'modzi mwa iwo anali ngati Mwana wa Mulungu. ***(3: 19-25)***<br>5. Ayudawo sanavulazidwe! Mfumu inakondwera kwambiri ndipo sinalolenso wina aliyense kuti aziyankhula zoyipa za Mulungu wa Ayuda. Iyo inakwezanso pa udindo anyamata amenewa ngakhale kuti anakana kumumvera! ***(3: 28-30)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Ng'anjo yamoto. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Sadrake, Mesake ndi Abedinego anakana kupembedza fano limenelo. ***(3: 12)***<br>2. Nebukadinezara anakwiya nawo ndipo anaopseza kuti awaponya m'ng'anjo yamoto. ***(3: 15)***<br>3. Sadrake, Mesake ndi Abedinego anawuza Nebukadinezara kuti ngakhale atawaponya m'ng'anjo yamoto, Mulungu angathe kuwapulumutsa. ***(3: 17)***<br>4. Pamenepo Nebukadinezara analamulira kuti ng'anjo ayitenthetse kasanu ndi kawiri kuposa nthawi zonse ndipo awaponyemo anyamata atatu a Chihebri. Ng'anjo inatentha kwambiri motero kuti anthu amene anaponya anyamatawo anaphedwa ndi motowo. Koma pamene mfumu inayang'anamo, inadabwa kuona anthu anayi – m'modzi mwa iwo anali ngati Mwana wa Mulungu. ***(3: 19-25)***<br>5. Ayudawo sanavulazidwe! Mfumu inakondwera kwambiri ndipo sinalolenso wina aliyense kuti aziyankhula zoyipa za Mulungu wa Ayuda. Iyo inakwezanso pa udindo anyamata amenewa ngakhale kuti anakana kumumvera! ***(3: 28-30)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kukhala mbali ya Mulungu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Kambiranani ndi ana momwe Vesi Yoloweza ikufotokozera mwachidule zochitika zonse za m'phunziro lino.<br><br>Onaninso pa ***Yohane 10: 28*** ndi kukambirana lonjezo lalikulu limene Ambuye Yesu anachita kwa amene amamutsatira. | 1. ***Eksodo 20: 1-6*** – Werengani ndi kukambirana zomwe akunena za kusapembedza mafano. Sadrake, Mesake ndi Abedinego anamvera zimenezi. Yankhulani za kufunika kwa kudziwa zomwe Baibulo limaphunzitsa za kukondweretsa Mulungu.<br>2. ***Machitidwe 5: 27-32*** – Werengani ndi kukambirana momwe Petro ndi atumwi, monga anyamata awa, anawuza Mkulu wa Ansembe ndi Bwalo Lalikulu kuti iwo adzamvera Mulungu osati anthu. ***(vesi 29)*** |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ngati ndife Akhristu tikuyenera kuphunzira kuchokera m'phunziro limeneli kuti Ambuye Yesu angathe kutithandiza pa mavuto kapena kukhala nafe m'mavutowo.<br>2. Monga momwe mfumu inakhutira ndi zochiza za anyamata awa pa kukhulupirika kwa Mulungu wawo, moteronso amene si Akhristu akuyenera kukhutira ndi moyo wa Akhristu komanso chikhulupiriro chawo.<br>3. Sadrake, Mesake ndi Abedinego anali okonzeka kukhala okhulupirika kwa Mulungu ngakhale atakumana ndi zovuta. Monga Akhristu tikuyenera kukonzekera kukhala moyo monga umenewu lero. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Chikhulupiriro cha anyamata atatu amenewa chinali chapadera. Chimatchedwa chikhulupiriro cha 'atapanda'. Iwo anati, "Mulungu wathu akhoza kutipulumutsa ife, ***koma atapanda kutero***, ife tikukanabe kugwada." Pemphani Mulungu kuti akupatseni chikhulupiriro ngati chimenechi. ***(Ahebri 11: 1)***<br>2. Sadrake, Mesake ndi Abedinego anali abwenzi ndipo analimbikitsana pa nthawi ya mayesero. Onetsani kuti mukulimbikitsana ndi amene amakonda Ambuye Yesu. |

| | C1 – KALASI 3<br>Phunziro Lachitatu – Danieli<br>Mutu – Dzanja lodabwitsa | C1 – KALASI 4<br>Phunziro Lachitatu – Danieli<br>Mutu – Kuyankhulira Mulungu |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Danieli 5: 1-31***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Danieli 5: 23***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mfumu Belisazara, monga abambo ake Nebukadinezara, sanalabadire Mulungu pa machitidwe awo.<br>2. N'kwapafupi kuyiwala zonse zimene makolo anatiphunzitsa komanso kuyiwala maphunziro amene timaphunzira m'Baibulo. | **Werengani:** ***Danieli 5: 1-31***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Danieli 5: 23***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mfumu Belisazara inali yonyada ndipo sinkalabadira za Mulungu monga abambo ake Nebukadinezara.<br>2. Mulungu amalamulira chilichonse ndipo tikuyenera kumudalira ndi kumumvera. |
| **MAWU OYAMBA** | Taganizirani malamulo ena amene tili nawo m'dziko lathu kapena pa sukulu pathu. Tayesani kulemba uthenga wamphamvu wa mawu osaposera ANAYI. Kambiranani zotsatira zake zitha kukhala zotani. Chitsanzo: Musathamange pa sukulu! | Ganizirani za zolamulira ndi malamulo a m'dziko lanu. Kambiranani zotsatira zake ngati sitilabadira malamulo amenewo ndi chifukwa chomwe wophwanya lamulo akuyenera kulangidwa. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mfumu Belisazara inali ndi phwando lalikulu la nduna zake 1,000. Iyo sinalabadire maphunziro amene abambo ake anaphunzira za kutsatira Mulungu. Iyo inalamula kuti agwiritse ntchito ziwiya zasiliva ndi zagolide za m'nyumba ya Mulungu ku Yerusalemu. ***(5: 1-2)***<br>2. Mwadzidzidzi kunaoneka zala za munthu zikulemba uthenga pa khoma. Mfumu inachita mantha kwambiri. Panalibe amene ankadziwa kuti mawu amatanthauza chiyani. ***(5: 5-9)***<br>3. Anabwera ndi Danieli monga munthu yekhayo amene akanatha kumasulira zolembedwa pa khomazo. ***(5: 10-16)***<br>4. Danieli anafotokoza kuti Mulungu akuwuza mfumu kuti sinaphunzire pa zimene zinachitikira abambo ake. Iyo sinkapereka ulemu kwa Mulungu amene amasunga moyo wake m'manja mwake ndi zochita zake zonse! *Mulungu amasunga miyoyo yathu ndi njira zathu zonse m'manja mwake, monga mfumu ija.* ***(5: 17-28)***<br>5. Mulungu analanga Belisazara ndipo anafa usiku omwewo, komanso ufumu wake unagawikana. Dariyo, m'Medi anakhala wolamulira. ***(5: 30-31)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Dzanja lodabwitsa. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mfumu Belisazara inali ndi phwando lalikulu la nduna zake 1,000. Iyo sinalabadire maphunziro amene abambo ake anaphunzira za kutsatira Mulungu. Iyo inalamula kuti agwiritse ntchito ziwiya zasiliva ndi zagolide za m'nyumba ya Mulungu ku Yerusalemu. ***(5: 1-2)***<br>2. Belisazara ndi abwenzi ake sanaonetse ulemu kwa Mulungu ndi chuma chake cha m'Nyumba yake. M'malo mwake iwo ankapembedza mafano.<br>3. Mwadzidzidzi kunaoneka zala za munthu zikulemba uthenga pa khoma. Mfumu inachita mantha kwambiri. Panalibe amene ankadziwa kuti mawu amatanthauza chiyani. ***(5: 5-9)***<br>4. Anabwera ndi Danieli monga munthu yekhayo amene akanatha kumasulira zolembedwa pa khomazo. ***(5: 10-16)***<br>5. Danieli anafotokoza kuti Mulungu ankawuza mfumu kuti sinaphunzire kuchokera pa zomwe zinachitikira abambo ake. Komanso, sankakondwera ndi zisankho zake, makhalidwe ake ndi zochita zake.<br>6. Iyo sinkapereka ulemu kwa Mulungu amene amasunga moyo wake m'manja mwake ndi zochita zake zonse! *Mulungu amasunga miyoyo yathu ndi njira zathu zonse m'manja mwake, monga mfumu ija.* ***(5: 17-28)***<br>7. Mulungu analanga Belisazara ndipo anafa usiku omwewo, komanso ufumu wake unagawikana. Dariyo m'Medi ndiye anakhala wolamulira. ***(5: 30-31)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjera A – Kuyankhulira Mulungu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Jambulani chinthu chooneka monga kangaude ndi kulemba mauthenga kusonyeza momwe Mulungu amayankhulira ndi anthu lero. | Kambiranani m'magulu kenaka bwerani ndi zimene mwakambirana pa gulu lonse:<br>1. Kodi chimachititsa anthu kusalabadira za Mulungu ndi chiyani?<br>2. Kodi tidziyembekezera chilango chotani ngati sitilabadire za Mulungu? |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi Mulungu amayankhula nafe lero? M'njira zotani?<br>2. Kodi ife sitinalabadire za Mulungu ndi njira zake monga Belisazara?<br>3. Kodi n'kofunika kuti tivomereze machimo athu ndi kupempha Mulungu kuti atikhululukire? Werengani ***Aroma 6: 23***. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Mulungu akufuna kuti ife timulole akhale woyamba m'miyoyo yathu.<br>2. Kodi tingachite chiyani chomwe chidzakondweretsa Mulungu? Onani pa ***Mateyu 6: 33 ndi Ahebri 11: 6***. |

| | **C1 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachinayi – Danieli**<br>**Mutu – Dzenje la mikango** | **C1 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachinayi – Danieli**<br>**Mutu – Kuvutika chifukwa cha Mulungu** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Danieli 6: 1-28***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Danieli 6: 23***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Danieli anali wokhulupirika pamaso pa Mulungu ngakhale ankakumana ndi masautso.<br>2. Akhristu amadziwa kuti amakhala ndi Mulungu nthawi zonse ngakhale pamene akudutsa m'masautso ambiri. | **Werengani:** ***Danieli 6: 1-28***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Danieli 6: 23***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Danieli anali wokhulupirika pamaso pa Mulungu ngakhale ankakumana ndi masautso.<br>2. N'kofunika kwambiri kuti Mulungu azikhala woyamba m'miyoyo yathu ngakhale tikukumana ndi zinthu zovuta. |
| **MAWU OYAMBA** | Ganizirani zitsanzo kuchokera m'Baibulo kapena mu mbiri za munthu amene anayima pa chimene ankakhulupirira ndipo zotsatira zake anapeza mavuto. | Kodi anthu amene amatsatira Yesu angakumane ndi zotchinga zotani? Ngati mungathe, fufuzani pa - www.opendoorsuk.org |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mfumu Dariyo ndiye anali wolamulira Babulo tsopano. Danieli anali ndi udindo wofunika kwambiri wolamulira. Mfumu inkakonda Danieli ndipo inkamulemekeza chifukwa ankapambana pa chilichonse chimene ankachita. ***(6: 1-3)***<br>2. Akalonga kapena nduna zina zinamuchitira nsanje ndipo zinakonza chiwembu choti Danieli akhale pa mavuto. Iwo anakakamiza Mfumu Dariyo kuti aliyense azigwada ndi kupembedza iye yekha kwa masiku makumi atatu. ***(6: 4-9)***<br>3. Danieli anapitiriza tsiku lililonse kupita mu chipinda chake kukapemphera kwa Mulungu katatu pa tsiku. ***(6: 10)***<br>4. Anakawuza mfumu zimenezi. Mfumu inayesera kuti isinthe lamulo lake lomwelo koma inalephera. Mfumu inalibe njira ina koma kuponya Danieli m'dzenje la mikango. ***(6: 11-17)***<br>5. *Danieli anadalira Mulungu ndipo anakonzeka kuti kupemphera kwa Mulungu wake kukhale koposa moyo wake. Danieli ankakhulupirira kuti Mulungu ankalamulira ndipo adzamuteteza m'dzenje la mikango.*<br>6. Mfumu, kudandaula za Danieli, inalephera kugona usiku wonse, koma inakondwera pamene inaona kuti Danieli ali moyo ndipo ali bwino m'mawa mwake. Mulungu anatseka pakamwa pa mikango! ***(6: 18-23)***<br>7. Amene anakonza chiwembu aja anaponyedwa m'dzenje la mikango ndipo anadyedwa nthawi yomweyo. ***(6: 24)***<br>8. Mfumu Dariyo inalamula kuti aliyense aziwopa ndi kupereka ulemu kwa Mulungu wa Danieli. ***(6: 25-27)*** *Fotokozani mosavuta tanthauzo la zimenezi.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Dzenje la mikango. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Mfumu Dariyo ndiye anali wolamulira Babulo tsopano. Danieli anali ndi udindo wofunika kwambiri wolamulira. Mfumu inkakonda Danieli ndipo inkamulemekeza chifukwa ankapambana pa chilichonse chimene ankachita. ***(6: 1-3)***<br>2. Akalonga kapena nduna zina zinamuchitira nsanje ndipo zinakonza chiwembu choti Danieli akhale pa mavuto. Iwo anakakamiza Mfumu Dariyo kuti aliyense azigwada ndi kupembedza iye yekha kwa masiku makumi atatu. ***(6: 4-9)***<br>3. Danieli anapitiriza tsiku lililonse kupita mu chipinda chake kukapemphera kwa Mulungu katatu pa tsiku. ***(6: 10)***<br>4. Anakawuza mfumu zimenezi. Mfumu inayesera kuti isinthe lamulo lake lomwelo koma inalephera. Mfumu inalibe njira ina koma kuponya Danieli m'dzenje la mikango. ***(6: 11-16)***<br>5. *Danieli anadalira Mulungu ndipo anakonzeka kuti kupemphera kwa Mulungu wake kukhale koposa moyo wake. Danieli ankakhulupirira kuti Mulungu ankalamulira ndipo adzamuteteza m'dzenje la mikango.*<br>6. Mfumu, kudandaula za Danieli, inalephera kugona usiku wonse, koma inakondwera pamene inaona kuti Danieli ali moyo ndipo ali bwino m'mawa mwake. Mulungu anatseka pakamwa pa mikango! Kenaka Danieli anatulutsidwa. ***(6: 18-23)***<br>7. Amene anakonza chiwembu aja anaponyedwa m'dzenje la mikango ndipo anadyedwa nthawi yomweyo. ***(6: 24)***<br>8. Mfumu Dariyo inalamula kuti aliyense aziwopa ndi kupereka ulemu kwa Mulungu wa Danieli. ***(6: 25-27)*** *Fotokozani mosavuta tanthauzo la zimenezi.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kuvutika chifukwa cha Mulungu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Kambiranani m'magulu kenaka bwerani pa gulu lonse ndi kufotokoza:<br>Kodi ndi m'njira ziti zomwe Akhristu atha kunyozedwa chifukwa cha Mulungu pa sukulu?<br>Kodi nkhani ya Danieli ikutithandiza motani za mmene tingachitire ndi zimenezi? | Kambiranani m'magulu kenaka bwerani pa gulu lonse ndi kufotokoza:<br>Palibe amene amafuna mavuto. Kodi mavuto omwe anachitikira Danieli anamukhudza motani?<br>Pamene tikukumana ndi mavuto tikuyenera kuchita chiyani? |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>N'chifukwa chiyani sitikuyenera kuchita mantha kukhala mbali ya Mulungu?<br>Werengani ***Yoswa 1: 9***.<br>Kodi izi zikutanthauza kuti sadzakumana ndi mavuto ena aliwonse? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Danieli anali ndi chizolowezi chopemphera katatu pa tsiku. Kodi pa nkhani imeneyi tingaphunzire chiyani chomwe chingakhale chothandiza pa miyoyo yathu ya Chikhristu?<br>2. M'magulu, thandizanani kuyerekeza ndi pemphero lotani limene Danieli ankapemphera nthawi iliyonse imene walowa mu chipinda. |

| | C2 – KALASI 3<br>**Phunziro Loyamba – Yesu akumana ndi munthu ku Yeriko**<br>**Mutu – Yesu ndi kukhululukira** | C2 – KALASI 4<br>**Phunziro Loyamba – Zoyankhula za Yesu**<br>**Mutu – Za tchimo** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Luka 19: 1-10***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 19: 10***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu anakumana ndi munthu wotchedwa Zakeyu - wamisonkho wosasangalala ndi wachinyengo.<br>2. Moyo wa Zakeyu unasintha pamene anakumana ndi Yesu. | **Werengani:** ***Luka 19: 1-10***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 19: 10***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kukumana ndi Yesu chinali chinthu chopambana kwambiri chimene sichinachitikepo kwa Zakeyu.<br>2. Zakeyu sanalinso chimodzimodzi kuyambira tsiku limeneli. Moyo wake unasintha. |
| **MAWU OYAMBA** | Fotokozani kuti mnzanu ankachita chinyengo pa masewero ake ndi inu. Kodi munachita chiyani ndi amene sankatsatira malamulo?<br>Phunziro la lero ndi la munthu amene sanali wotchuka chifukwa anali wachinyengo. Anthu ankaganiza kuti anali woyipa koma Yesu anaonetsa chikondi kwa iye ndipo anafuna kukumana naye. | Zakeyu sanali munthu wotchuka. Kodi alipo anthu osatchuka m'kalasi mwanu kapena pa sukulu?<br>Kodi ndi zinthu ziti zomwe zimawachititsa kukhala osatchuka?<br>Kodi inu mungaonetse motani chikondi monga mmene anachitira Yesu kwa anthu ambiri a makhalidwe osiyanasiyana? |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Zakeyu anali ndi chuma koma anali wosatchuka chifukwa ankagwira ntchito yolandira misonkho ya Aroma. ***(19: 1-2)*** Iye nthawi zina ankachita chinyengo potenga ndalama zoposa zomwe ankayenera kutenga.<br>2. Zakeyu ankafuna kuona Yesu pamene Iye anabwera ku Yeriko ndipo anakwera mu mtengo kuti amuone chifukwa anali wamfupi msinkhu! ***(19: 3-4)***<br>3. Yesu anawuza Zakeyu kuti atsike mu mtengo ndi kuti akufuna kupita ku nyumba ya Zakeyu. ***(19: 5-6)***<br>4. Zakeyu anamulandira Yesu m'nyumba mwake koma anthu sanakondwere ndi zimenezi.<br>5. Zakeyu anamva chisoni chifukwa cha machimo ake ndipo anawuza Yesu kuti apereka ndalama zake kwa osauka ndiponso kwa anthu amene anawabera. ***(19: 8)***<br>6. Yesu anati chipulumutso chafika m'nyumba mwa Zakeyu. ***(19: 9)***<br>7. Yesu anati anabwera kudzafunafuna ndi kupulumutsa anthu otayika monga Zakeyu. Iyi ndi nkhani yabwino! ***(19: 10)*** *Fotokozani kuti izi zikutanthauza chiyani kwa achinyamata lero.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A - Yesu ndi kukhululukira. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Zakeyu anali ndi chuma koma anali wosatchuka chifukwa ankagwira ntchito yolandira misonkho ya Aroma. ***(19: 1-2)*** Anthu sankakhulupirira olandira misonkho ndipo ankatenga Zakeyu kukhala munthu wopereka anzake. Iye nthawi zina ankachita chinyengo potenga ndalama zoposa zomwe ankayenera kutenga.<br>2. Zakeyu ankafuna kuona Yesu pamene Iye anabwera ku Yeriko ndipo anakwera mu mtengo kuti amuone chifukwa anali wamfupi msinkhu! ***(19: 3-4)***<br>3. Yesu ankadziwa chimene Zakeyu anali ndi kumene anali. Yesu ankadziwa chilichonse cha iye. Yesu anawuza Zakeyu kuti atsike mu mtengo ndi kuti akufuna kupita ku nyumba yake. ***(19: 5-6)***<br>4. Zakeyu analandira Yesu m'nyumba mwake koma anthu sanakondwere ndi zimenezi chifukwa Yesu ankapita ku nyumba ya munthu wosatchuka ngati ameneyu.<br>5. Zakeyu anamva chisoni ndi khalidwe lake lauchimo ndipo anafuna kukonza zinthu. Iye anapereka ndalama zake kwa osauka ndi kwa aliyense amene anamubera. ***(19: 8)***<br>6. Yesu anati chipulumutso chafika m'nyumba ya Zakeyu. ***(19: 9)***<br>7. Yesu anati anabwera kudzafunafuna ndi kupulumutsa anthu otayika monga Zakeyu. Iyi ndi nkhani yabwino! ***(19: 10)***<br>8. *Pamene talapa, tikuyenera kumva chisoni chifukwa cha machimo athu komanso kutembenuka mtima ndi kupereka miyoyo yathu kwa Mulungu; pamenepo n'kotheka kukonzanso zinthu zolakwika. Ngati timupempha Iye, Ambuye Yesu adzatipulumutsa ndi kutithandiza kukhala moyo wathu ndi Mulungu.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Za tchimo. |
| **KUKUMBUTSANA** | Awiriawiri, yerekezani kuti mukufunsa mafunso Zakeyu pa wailesi kapena pa kanema za tsiku limene anakumana ndi Yesu ndi momwe anasinthira moyo wake. Konzani mafunso ndi mayankho. M'modzi akhale wofunsa mafunso ndipo winayo akhale Zakeyu. Kumbukirani kufunsa mafunso molingana ndi nkhani ya ***Luka 19: 1-10***. | Munthu pa yekha kapena awiriawiri, yerekezani kuti ndinu Zakeyu. Lembani nkhani yachidule ya tsiku limene munakumana ndi Yesu ndi momwe zinasinthira moyo wanu. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi anthu akuyenera kukhala angwiro kapena otchuka kuti Mulungu asinthe miyoyo yawo? Ayi! Zakeyu anali wosatchuka ndi wochimwa, koma Yesu anamusintha.<br>2. Pakuti Yesu anabwera kudzafunafuna ndi kupulumutsa otayika, kodi Akhristu akhale motani ndi anthu 1) wosatchuka? 2) wochimwa? 3) amene sakhulupirira Mulungu? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi kutsatira Yesu kukuyenera kusintha motani miyoyo yathu a) ku nyumba, b) ku sukulu, c) mu mpingo?<br>2. Kutsatira chitsanzo cha Yesu, kodi Akhristu akuyenera kukhala nawo motani anthu amene ndi osatchuka kapena amene satsatira malamulo a m'Baibulo? |

| | C2 – KALASI 3 | C2 – KALASI 4 |
|---|---|---|
| | **C2 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachiwiri – Yesu akumana ndi amayi pa chitsime**<br>**Mutu – Yesu ndi madzi a moyo** | **C2 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachiwiri – Zoyankhula za Yesu**<br>**Mutu – Za kuona** |
| | **Werengani:** ***Yohane 4: 5-30***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 4: 29***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu anakumana ndi mayi pa chitsime amene ankanyozedwa ndi kukhala yekha.<br>2. Yesu amakonda, amadziwa ndipo atha kuthandiza aliyense. | **Werengani:** ***Yohane 9: 1-41***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 9: 5***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu anakumana ndi munthu wosaona ndi kumuchiritsa.<br>2. Anthu amene satsatira Ambuye Yesu ali ndi khungu lauzimu. Ndi Yesu yekha angawapatse kuwona kwenikweni. |
| **MAWU OYAMBA** | Kambiranani zokathamanga kapena kuyenda mtunda wautali kukutentha. Kodi mungamve ludzu? Kodi mungamve bwanji ngati munthu wina atakupatsani chakumwa? Lembani mawu ofotokoza momwe mungamvere mu mtima ngati wina atakupatsa chakumwa chozizira pamene muli ndi ludzu kwambiri. | Mafunso okambirana pa gulu:<br>• Kodi mukudziwa anthu ena amene saona?<br>• Kodi moyo wawo ndi otani?<br>• Kodi moyo wawo ungasinthe motani ngati mwadzidzidzi atayamba kuonanso zinthu?<br>• Kodi amene akuona angathandize motani anthu amene sakuona? |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Pamene Yesu anayima pa ulendo wake odzera mu Samariya kupuma pa chitsime, anakumana ndi mayi wa Chisamariya. ***(4: 4-7)***<br>2. Ayuda sankagwirizana ndi Asamariya ndipo sankayankhulana nawo. Ambuye Yesu anali wosiyana. Iye amakonda aliyense kaya ndi ndani. Mayi anadabwa pamene Yesu anamupempha madzi akumwa. Monga mmene zinkachitikira, anthu a Chiyuda sakanayankhulana naye. ***(4: 7-9)***<br>3. Pamene Yesu anamuwuza kuti atha kumupatsa madzi a moyo, iye sanamvetsetse. ***(4: 10-14)***<br>4. Yesu ankadziwa za moyo ndi banja la mayi wa Chisamariya. Iye anaganiza kuti Yesu anali mneneri. ***(4: 17-19)***<br>5. Yesu anawuza mayiyu kuti Iye anali Mesiya amene abale ake ankamuyembekezera. ***(4: 26)***<br>6. Mayiyu anakhulupirira Yesu ndipo nthawi yomweyo anapita kukawuza anzake ndi anansi ake m'mudzimo. Iye anasiya mtsuko wake pa chitsime. Iye anapeza madzi a moyo amene Yesu yekha ndiye angapereke - moyo wosatha. ***(4: 28-30)***<br>7. *Fotokozani za kufunika kwa madzi m'matupi mwathu, koma Yesu ankayankhula za chosowa chathu chauzimu ndiye madzi a moyo.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Yesu ndi madzi a moyo. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yesu anakumana ndi munthu amene anabadwa wosaona. Ophunzira anafunsa ngati kusaona kwake chinali chilango cha Mulungu. Yesu anati adzamuchiritsa munthuyo kuti aliyense aone ntchito za Mulungu m'moyo mwake. ***(9: 1-3)***<br>2. Yesu anapaka matope m'maso mwa munthuyo ndi kumuwuza kuti apite akasambe ku dziwe la Siloamu. Munthuyo anamvera ndipo chodabwitsa chinachitika: anayamba kuona. ***(9: 6-7)***<br>3. Afarisi anawuzidwa za chodabwitsachi ndipo iwo anati Yesu sanali wochokera kwa Mulungu chifukwa anachiritsa munthu tsiku la Sabata. Iwo sankakhulupirira kuti Ambuye Yesu anali Mwana wa Mulungu. ***(9: 13-17)***<br>4. Munthu amene anali wosaona anazindikira kuti anali Yesu amene anachititsa kuti ayambe kuona. Iye anakhulupirira Ambuye Yesu kuti anali Mwana wa Mulungu ndipo anamupembedza. ***(9: 35-38)***<br>5. *Munthu wosaona anayamba kuona zinthu ndi maso ake pamene Ambuye Yesu anamuchiritsa, koma iye anazindikiranso kuti Yesu anali ndani ndipo anakhulupirira. Iye anayambanso kuona mwauzimu monganso ku thupi. Afarisi ankaona ku thupi koma ankakana kukhulupirira kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu. Iwo anali ndi khungu lauzimu.*<br>6. *Ambuye Yesu ndi Kuunika kwa Dziko Lapansi. Iye anabwera kuti ife tichiritsidwe ku khungu lauzimu.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Za kuona. |
| **KUKUMBUTSANA** | 1. Potsatira chitsanzo cha Yesu, kodi tikhale nawo motani anthu ena? Perekani chitsanzo.<br>2. Kodi mayi uja anachita chiyani Yesu atamuwuza kuti Iye ndi Mesiya? Chifukwa chiyani? Kodi zotsatira za zomwe anachita zinali zotani? | Khalani awiriawiri pa zokambirana. Werengani ndime ya m'Baibulo ndi kukambirana zotsatira za chodabwitsa cha:<br>a) Mnansi.<br>b) Makolo a munthu wosaona.<br>c) Afarisi.<br>d) Munthu amene anabadwa wosaona. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi inu munalandira "madzi a moyo" amene Ambuye Yesu amapereka? Kodi munakhulupirira Iye? Onani pa ***Yohane 7: 37-39.***<br>2. Kodi munawuzapo anthu ena za Iye? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Onani pa ***Yohane 8: 12*** ndi kukambirana momwe tingadziwire "kuunika kwa moyo" m'miyoyo yathu. |

| | C2 – KALASI 3<br>Phunziro Lachitatu – Yesu akumana ndi munthu usiku<br>Mutu – Yesu ndi kubadwa mwatsopano | C2 – KALASI 4<br>Phunziro Lachitatu – Zoyankhula za Yesu<br>Mutu – Za abusa |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Yohane 3: 1-16***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 3: 16***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu anakumana ndi Nikodemo, Mfarisi, amene ankafuna thandizo.<br>2. Yesu anamuwuza kuti ankayenera kubadwanso kuti alandire kuchokera kwa Mulungu mphatso ya moyo watsopano. Iyi imaperekedwa kwa ife ngati takhulupirira. | **Werengani:** ***Yohane 10: 1-33***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 10: 9***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu anaphunzitsa kuti ife tili ngati nkhosa ndipo Iye ali ngati M'busa amene amayang'anira ife.<br>2. Ngati timakhulupirira Iye, ndife nkhosa zake ndipo Iye monga M'busa sadzatikhumudwitsa. |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za kubadwa kwa mwana wakhanda. N'chifukwa chiyani imakhala nthawi ya chisangalalo? Ganizirani za moyo watsopano ndi kufunika kwa masiku obadwa ndi kupambana kwake. | Lembani ntchito zimene abusa aziweto amagwira (monga, kuteteza nkhosa, kutsogolera nkhosa, kufunafuna nkhosa ikasochera, kuzipatsa zakudya ndi madzi). |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Nikodemo anali mtsogoleri wa chipembedzo cha Chiyuda amene anabwera kudzaonana ndi Yesu usiku. Ife sitikudziwa chifukwa chake. Mwina ankachita manyazi kubwera kudzaonana ndi Yesu ndipo anaganiza zopita kuli mdima.<br>2. Nikodemo anati Yesu anali wochokera kwa Mulungu chifukwa palibe munthu akanatha kuchita zodabwitsa zimene ankachita popanda thandizo la Mulungu. ***(3: 1-2)***<br>3. Yesu anati palibe angathe kuona Ufumu wa Mulungu ngati sabadwanso mwatsopano. Nikodemo sanamvetsetse za kuti munthu wamkulu angathe kubadwanso ngati khanda. ***(3: 3-4)***<br>4. Yesu anati kuti munthu alowe mu Ufumu wa Mulungu akuyenera kubadwanso kuti alandire moyo wa Mulungu umene Mzimu amapereka. ***(3: 5-8)***<br>5. Iye anafotokozanso kwa Nikodemo kuti Iye adzapachikidwa pa mtanda, monga anachitira Mose m'chipululu popachika njoka yamkuwa pa mtengo. Ngati munthu wolumidwa ndi njoka ayang'ana njoka yamkuwa, sankafa koma ankachira. ***(Numeri 21: 4-9) (Yohane 3: 14)***<br>6. *Yesu anawuza Nikodemo kuti Mulungu anakonda dziko lapansi, kotero anapereka Mwana wake wobadwa yekha, Yesu. Yesu anapachikidwa pamene anafa pa mtanda. Aliyense amene atembenukira kwa Yesu ndi kumukhulupirira sadzafa koma adzakhala ndi moyo wosatha.* ***(Yohane 3: 16 - Vesi Yoloweza)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Yesu ndi kubadwa mwatsopano. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yesu anawuza Afarisi kuti Iye ndi M'busa ndipo ali ngati Khomo la nkhosa. Iye amatiteteza monga momwe m'busa amatetezera khomo la khola lake. ***(10: 7-11)*** Yesu anagwiritsa ntchito zithunzi izi pofuna kufotokoza zambiri za Iye mwini kwa anthu.<br>2. Yesu anati Iye, mosiyana ndi atsogoleri ena, anabwera kudzapereka moyo kwa anthu. ***(10: 10)***<br>3. Yesu anati Iye ndi M'busa Wabwino amene amataya moyo wake chifukwa cha nkhosa. ***(10: 11 ndi 14)***<br>4. Anthu ankaganiza kuti Yesu anali wamisala. Ena anakana kukhulupirira kuti Iye anali Mwana wa Mulungu. ***(10: 21 ndi 24-25)***<br>5. Yesu anawuza Ayuda kuti zinthu zazikulu zomwe ankachita zinkaonetsa kuti Iye anali Mesiya wochokera kwa Mulungu. Pamene iwo anamva izi, Ayuda ena anakana kumukhulupirira. Iwo anayesetsa kuti amuphe pogenda miyala. Anthu amenewa sanali nkhosa zake. ***(10: 31-33)***<br>6. Komabe anthu ena anakhulupirira Yesu. Anthu amenewa ndiye anali nkhosa zake.<br>7. Tikakhala tokha, tidzachoka pamaso pa Mulungu. Ife timafuna Ambuye Yesu kuti azititsogolera m'njira imene tikuyenera kuyenda ndi kutipatsa moyo wosatha. ***(10: 28) (Onani Yesaya 53: 6)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Za abusa. |
| **KUKUMBUTSANA** | Mafunso:<br>1. Kodi Yesu anati ndi chiyani chimene chikuyenera kuchitika poyamba kuti munthu aone Ufumu wa Mulungu?<br>2. Kodi Yesu anati Nikodemo ankayenera kukhalanso ngati khanda?<br>3. Kodi tikuyenera kulipira kuti Mulungu atipatse moyo watsopano?<br>4. Kodi chinkachitika ndi chiyani pamene odwala ankayang'ana njoka yamkuwa imene Mose anapachika m'chipululu? Chinkachitika n'chiyani ngati sayang'ana?<br>5. Kodi ife tichite chiyani kuti tilandire mphatso ya Mulungu ya moyo wosatha?<br>6. Kodi chidzachitika ndi chiyani tikakhulupirira Yesu? | Zokambirana pa gulu: Kodi Yesu ankatanthauza chiyani pamene ananena kuti Iye anali:<br>1. Khomo la nkhosa? ***(10: 9)***<br>2. M'busa Wabwino? ***(10: 11 ndi 14)*** |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Kodi munapempha Ambuye Yesu kuti akupatseni moyo watsopano wa Mulungu? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Onani mndandanda wa ntchito zimene m'busa amagwira. Kodi chimasintha ndi chiyani tikadziwa kuti Yesu ndiye M'busa wathu? |

| | C2 – KALASI 3<br>**Phunziro Lachinayi – Yesu akumana ndi munthu wosaona**<br>**Mutu – Yesu ndi kuunika** | C2 – KALASI 4<br>**Phunziro Lachinayi – Zoyankhula za Yesu**<br>**Mutu – Za chipulumutso** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Yohane 9: 1-38***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 9: 25***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu anakumana ndi munthu wosaona ndi kumuchiritsa.<br>2. Anthu amene satsatira Yesu ali ndi khungu lauzimu. Ndi Yesu yekha amene angatsekule maso awo. | **Werengani:** ***Yohane 3: 1-16***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 3: 16***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu anakumana ndi Nikodemo, Mfarisi (munthu wachipembedzo), amene ankafuna thandizo<br>2. Yesu anamuwuza kuti ankayenera kubadwanso kuti alandire mphatso ya Mulungu ya moyo watsopano. Umaperekedwa kwa ife ngati tikhulupirira Yesu. |
| **MAWU OYAMBA** | Kambiranani za kukumana ndi munthu wosaona. Kodi anthu osaona amakumana ndi mavuto otani? Awiriawiri, lembani zomwe amakumana nazo ndi kufananitsa ndi gulu lina. Ganizirani momwe anthu amene akuona angathandizire munthu wosaona. | Zokambirana za pa gulu kapena awiriawiri: Kubadwa kwa mwana watsopano ndi nthawi yachisangalalo. Chifukwa chiyani? Ganizirani za moyo watsopano ndi kufunika kwa masiku obadwa ndi kupambana kwake. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yesu anakumana ndi munthu amene anabadwa wosaona. Ophunzira ake anamufunsa ngati chinali chilango chochokera kwa Mulungu. Yesu anati adzamuchiritsa munthuyo kuti aliyense athe kuona ntchito za Mulungu m'moyo wake. ***(9: 1-3)***<br>2. Yesu anapaka matope m'maso mwa munthuyo ndipo anamuwuza kuti apite akasambe ku Dziwe la Siloamu. Munthuyo anamvera ndipo modabwitsa anayamba kuona. ***(9: 6-7)***<br>3. Afarisi anawuzidwa za chodabwitsa ichi ndipo anati Yesu sankachokera kwa Mulungu chifukwa anachiritsa munthuyo tsiku la Sabata. Iwo sankakhulupirira kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu. Munthu wosaona anati ankaganiza kuti Yesu anali mneneri. ***(9: 13-17)***<br>4. Munthu amene anali wosaonayo anazindikira kuti ndi Yesi amene anamuchiritsa kuti aziona. Iye anakhulupirira kuti Ambuye Yesu anali Mwana wa Mulungu ndipo anamupembedza. ***(9: 35-38)***<br>5. *Munthu wosaona ankatha kuona zinthu pamene Ambuye Yesu anamuchiritsa, komanso anazindikira chimene Yesu anali ndipo anamukhulupirira. Iye ankatha kuona kuuzimu ndi kuthupi komwe. Afarisi ankaona kuthupi koma anakana kukhulupirira kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu. Iwo anali a khungu kuuzimu.*<br>6. *Ambuye Yesu ndi Kuunika kwa Dziko Lapansi. Iye anabwera ndi cholinga choti tipulumutsidwe ku khungu lauzimu.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Yesu ndi kuunika. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Nikodemo anali mtsogoleri wa Chipembedzo cha Chiyuda amene anabwera kwa Yesu usiku. Ife sitikudziwa chifukwa chake. Mwina ankafuna kuti zokambirana zawo zikhale za chinsinsi.<br>2. Nikodemo anati Yesu anachokera kwa Mulungu chifukwa palibe munthu akanatha kuchita zomwe Iye ankachita popanda thandizo la Mulungu. ***(Yohane 3: 1-2)***<br>3. Yesu anati palibe amene angaone Ufumu wa Mulungu pokhapokha atabadwanso. Nikodemo sanamvetsetse momwe munthu wamkulu abadwanso ngati khanda. ***(3: 4)*** Yesu anafotokoza kuti kubadwa kwachiwiri kunkafotokoza za moyo wauzimu osati wathupi.<br>4. Yesu anati kuti anthu akalowe mu Ufumu wa Mulungu akuyenera kubadwanso kuti alandire mphatso ya Mulungu ya moyo watsopano. Moyo umenewu amapereka ndi Mzimu Woyera. ***(3: 5-8)***<br>5. Yesu anafotokozeranso Nikodemo kuti Iye anadzapachikidwa pa mtanda monga mmene Mose anapachikira njoka yamkuwa pa mtengo m'chipululu. Ngati anthu odwala amene alumidwa ndi njoka adzayang'ana pa njoka yamkuwa sadzafa koma adzachira. ***(Numeri 21: 4-9) (Yohane 3: 14)***<br>6. *Yesu anawuza Nikodemo kuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero anapereka Mwana wake, Yesu. Yesu anapachikidwa pamene anafa pa mtanda. Aliyense amene atembenukira kwa Yesu ndi kukhulupirira, sadzafa koma adzakhala ndi moyo wamuyaya.* ***(Yohane 3: 16 - Vesi Yoloweza)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Za chipulumutso. |
| **KUKUMBUTSANA** | Jambulani zithunzi za nkhani yathu ya lero.<br>Komanso mutha kukhala anthu awiriawiri ndi kujambula zomwe mupachike pa khoma. | Zokambirana pa gulu:<br>1. Kodi zokambirana za pakati pa Ambuye Yesu ndi Nikodemo zikutiphunzitsa chiyani za kukhala Mkhristu?<br>2. Kodi chimasinthika ndi chiyani m'moyo wathu pamene takhulupirira Yesu? |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi anthu awa akusiyana motani m'makhalidwe awo? a) munthu wosaona b) Mfarisi c) anansi d) makolo ake?<br>2. Ganizirani za zomwe mungayankhe kwa Ambuye Yesu. Kodi ndinu wokonzekeza monga munthu wosaona uja kukhulupirira Iye? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi munakhulupirira Yesu kuti atha kukupatsani moyo wosatha?<br>2. Kodi munabadwa mwatsopano? |

| | C3 – KALASI 3<br>**Phunziro Loyamba – Chodabwitsa cha machiritso**<br>**Mutu – Yesu athandiza munthu wodwala** | C3 – KALASI 4<br>**Phunziro Loyamba – Mphamvu ya Ambuye**<br>**Mutu – Kuchiritsa wodwala** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Yohane 5: 1-16***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 5: 9***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu anakumana ndi munthu amene anakhala zaka zambiri akudwala.<br>2. Munthu sankatha kudzichiritsa. Ndi Yesu yekha amene akanachita zimenezo. | **Werengani:** ***Yohane 5: 1-16***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 5: 24***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu ndi wamphamvu ndi wokoma mtima. Iye ndi wachifundo ndipo amadalitsa anthu pamene amudalira osati chifukwa amamvera malamulo ena.<br>2. N'kofunika kumudalira Mulungu ndi kukhulupirira Ambuye Yesu kuposa kutsatira malamulo achipembedzo ndi miyambo yake. |
| **MAWU OYAMBA** | Munthu mu nkhani yathu ya lero anakhala akudikira kwa zaka 38 kuti achiritsidwe. Werengetsani kuti ndi masiku angati pa zaka 38. Fufuzani zinthu zina zimene zinachitika zaka 38 zapitazo kuti mukhale ndi chidziwitso cha kutalika kwa nthawi. | Mu nkhani iyi, Ayuda ankazunza Ambuye Yesu posachita zinthu mu njira imene iwo ankaganiza kuti ankayenera kutero.<br>Njira za Mulungu zimakhala zosiyana ndi njira zathu, koma tikuyenera kumvera m'malo motsatira maganizo athu. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yesu ali pa dziko lapansi, anthu ambiri ankagona m'mbali mwa dziwe la mu Yerusalemu lotchedwa Betesda. Iwo ankayembekezera kuchiritsidwa madzi akavunduka. ***(5: 1-3)***<br>2. Tsiku lina la Sabata, Yesu anaona munthu amene anakhala akudikira kwa zaka 38! Yesu anamufunsa ngati ankafuna kuchiritsidwa. ***(5: 5-6)***<br>3. Munthuyo anafotokoza kuti analibe wina woti akanamuthandiza kulowa m'dziwemo kuti achiritsidwe. Wina ankalowa iye asanalowe. Yesu anawuza munthuyo kuti ayimirire, anyamule mphasa yake ndipo aziyenda. Munthuyo anayimirira nthawi yomweyo. Yesu anachiritsa munthuyo! ***(5: 7-9)***<br>4. Munthuyo sanadziwe kuti anamuchiritsa ndi ndani. Tsiku lina, Yesu anamuona munthuyo ali mu Nyumba ya Mulungu. Munthuyo atazindikira amene anamuchiritsa, anapita kukawuza anthu kuti anali Yesu amene anamuchiritsa. ***(5: 14-15)***<br>5. Ayuda anamunena Yesu chifukwa anachiritsa munthu tsiku la Sabata. Iwo ankakhulupirira kuti munthu asagwire ntchito iliyonse pa Sabata. Iwo sanamvetsetse kapena kuvomereza kuti Yesu ankagwira ntchito ya Mulungu. ***(5: 16)***<br>6. *Fotokozani kuti Yesu sankangochiritsa kokha anthu nthawi imeneyo komanso lero angathe kupulumutsa aliyense amene angabwere kwa Iye ndi kumukhulupirira.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Yesu athandiza munthu wodwala. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yesu ali pa dziko lapansi, anthu ambiri ankagona m'mbali mwa dziwe la mu Yerusalemu lotchedwa Betesda. Iwo ankayembekezera kuchiritsidwa madzi akavunduka. ***(5: 1-3)***<br>2. Tsiku lina la Sabata, Yesu anaona munthu amene anakhala akudikira kwa zaka 38! Yesu anamufunsa ngati ankafuna kuchiritsidwa. ***(5: 5-6)***<br>3. Munthuyo anafotokoza kuti analibe wina woti akanamuthandiza kulowa m'dziwemo kuti achiritsidwe. Wina ankalowa iye asanalowe. Yesu anawuza munthuyo kuti ayimirire, anyamule mphasa yake ndipo aziyenda. Munthuyo anayimirira nthawi yomweyo. Yesu anachiritsa munthuyo! ***(5: 7-9)***<br>4. Munthuyo sanadziwe kuti anamuchiritsa ndi ndani. Tsiku lina, Yesu anamuona munthuyo ali mu Nyumba ya Mulungu. Munthuyo atazindikira amene anamuchiritsa, anapita kukawuza anthu kuti anali Yesu amene anamuchiritsa. ***(5: 14-15)***<br>5. Ayuda anamunena Yesu chifukwa anachiritsa munthu tsiku la Sabata. Iwo ankakhulupirira kuti munthu asagwire ntchito iliyonse pa Sabata. Iwo sanamvetsetse kapena kuvomereza kuti Yesu ankagwira ntchito ya Mulungu. ***(5: 16)***<br>6. *Fotokozani kuti Yesu sankangochiritsa kokha anthu nthawi imeneyo komanso lero angathe kupulumutsa aliyense amene angabwere kwa Iye ndi kumukhulupirira.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kuchiritsa wodwala. |
| **KUKUMBUTSANA** | Ana atha kulemba nkhani yayifupi ya mu nyuzi ya zomwe zinachitika mu nkhani ya lero. Iwo asankhe mutu wabwino wa nkhani zawo. Mukhala ndi khoma limene amate zomwe kalasi yalemba. | Lembani nkhani zazifupi ziwiri: imodzi ya munthu amene anachiritsidwa ndipo ina ya Ayuda amene sanasangalatsidwe kuti Ambuye Yesu anachiritsa munthu tsiku la Sabata. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Yesu anathandiza munthu amene anali ndi chosowa. Kodi ife tingathandize bwanji anthu amene ali ndi zosowa?<br>2. Ambuye Yesu atha kutipulumutsa nthawi yomweyo ngati tikhulupirira ndi kudalira Iye. Onani pa ***Machitidwe 16: 31*** ndi kuona kufunika kwake kwa aliyense. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Unikani maganizo osiyanasiyana pa Ambuye.<br>2. Kodi inu munamukhulupirira kapena mumayesa kukondweretsa Mulungu posunga malamulo?<br>3. Molingana ndi nkhaniyi, kodi njira ya Mulungu ndi iti? |

| | C3 – KALASI 3<br>Phunziro Lachiwiri – Chodabwitsa cha moyo<br>Mutu – Yesu athandiza munthu wachisoni | C3 – KALASI 4<br>Phunziro Lachiwiri – Mphamvu ya Ambuye<br>Mutu – Kuukitsa wakufa |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Marko 5: 21-43***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Marko 5: 42***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu anakumana ndi munthu amene mwana wake wamkazi ankadwala kwambiri ndipo palibe amene akanatha kumuthandiza.<br>2. Yesu sanangoonetsa kuti anali ndi mphamvu pa matenda pokha komanso pa imfa. | **Werengani:** ***Luka 8: 40-56***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 11: 25***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu anakumana ndi munthu amene mwana wake wamkazi ankadwala kwambiri ndipo palibe amene akanatha kumuthandiza.<br>2. Yesu sanangoonetsa kuti anali ndi mphamvu pa matenda pokha komanso pa imfa. |
| **MAWU OYAMBA** | Fotokozani kumene nkhani yayambira. Yairo anali mtsogoleri wa sunagoge kumene Ayuda ankasonkhana kumapembedza ngati alephera kupita ku Nyumba ya Mulungu ku Yerusalemu Iye ndiye ankatsogolera chipembedzo kumeneko, kuphunzitsa maphunziro a pakati pa sabata ndi kusamalira nyumbayo. Ambiri mwa atsogoleri a masunagoge anali pa ubale ndi Afarisi amene ankafuna kupha Yesu. Iye anabwera kwa Yesu chifukwa ankafunitsitsa thandizo. | Fotokozani kumene nkhani yayambira. Yairo anali mtsogoleri wa sunagoge. Ambiri mwa atsogoleri a masunagoge anali pa ubale ndi Afarisi amene ankafuna kupha Yesu. Iye anabwera kwa Yesu chifukwa ankafunitsitsa thandizo. Anthu monga mayi amene anali ndi nthenda yosachizika ankatengedwa kuti anali odetsedwa ndi Aphunzitsi. Anthu ankawatsala koma Yesu anafika kwa iwo ndi kuwathandiza. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yairo anafika kwa Yesu ndi kudzamudandaulira kuti apite naye kuti akachiritse mwana wake wamkazi. Yesu nthawi yomweyo anavomera ndi kunyamuka kupita ku nyumba ya Yairo. ***(5: 22-24)***<br>2. Ali m'njira yopita ku nyumba komwe kunali mwanayo, Yesu anachedwa ndi mayi amene anakhala akudwala kwa zaka khumi ndi ziwiri ndipo panalibe munthu amene akanatha kumuchiza. ***(5: 25-26)*** Mwachikhulupiriro, mayiyo anakhudza chovala cha Yesu ndipo anachiritsidwa. Yesu anamuwuza kuti afotokoze pa gulu zomwe zinachitikazi. ***(5: 27-34)*** Yesu sanakwiye naye koma anayamikira chikhulupiriro chake ndipo anamuwuza kuti apite kwawo mwamtendere.<br>3. Yesu akupita ku nyumba ya Yairo, Yairo analandira uthenga wa kuti mwana wake uja wamwalira koma Yesu anamulimbikitsa kuti asachite mantha koma akhulupirire. ***(5: 35-36)*** Yesu atafika ku nyumba ya Yairo anapeza anthu ambiri akulira koma Yesu anatulutsa onse.<br>4. Ndi ophunzira ake atatu ndi makolo a mwanayo, Yesu anaukitsa mwanayo. Iwo anadabwa kwambiri pamene mwanayo anayimirira, kuyamba kuyenda ndi kudya! Ndi Yesu yekha amene anamupatsa moyo! ***(5: 41-43)***<br>5. *Yesu anaonetsa mphamvu yake yayikulu pa matenda pamene anachiritsa mayi amene anakumana naye mu msewu ndiponso mphamvu yake pa imfa pamene anaukitsa mtsikana uja.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Yesu athandiza munthu wachisoni. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Chinali chachilendo kuona mtsogoleri wa sunagoge wolemekezeka monga Yairo kugwa pansi pa mapazi a Yesu ndi kumupempha kuti akachiritse mwana wake wamkazi! ***(Luka 8: 40-42)***<br>2. Ali m'njira yopita ku nyumba komwe kunali mwanayo, Yesu anachedwa ndi mayi amene anakhala akudwala kwa zaka khumi ndi ziwiri. Yesu anazindikira kuti mayiyo anamukhudza ndi cholinga. Ndipo anafuna kumuphunzitsa kuti sichinali chovala chake koma chikhulupiriro pa Iye ndiye chinamuchiritsa. Komanso anafuna kuphunzitsa Ayuda amene anali pamenepo amene ankamusala chifukwa cha matenda ake. Yesu sanakwiye naye koma anayamikira chikhulupiriro chake ndipo anamuwuza kuti apite kwawo mwamtendere. ***(8: 43-48)***<br>3. Yesu akupita ku nyumba ya Yairo, Yairo analandira uthenga wa kuti mwana wake uja wamwalira. Yesu anamulimbikitsa kuti asachite mantha koma akhulupirire ndipo anapita ku nyumba yake. ***(8: 49-50)*** Yesu atafika ku nyumba ya Yairo anapeza anthu ambiri akulira koma Yesu anatulutsa onse.<br>4. Ndi ophunzira ake atatu ndi makolo a mwanayo, Yesu anaukitsa mwanayo. Iwo anadabwa kwambiri pamene mwanayo anayimirira, kuyamba kuyenda ndi kudya! Ndi Yesu yekha amene anamupatsa moyo! ***(8: 51-56)***<br>5. *Yesu anaonetsa mphamvu yake yayikulu pa matenda pamene anachiritsa mayi amene anakumana naye mu msewu ndiponso mphamvu yake pa imfa pamene anaukitsa mtsikana uja.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kuukitsa wakufa. |
| **KUKUMBUTSANA** | Bwerezani ndi kukambirana za anthu anayi mu nkhaniyi:<br>1. Bambo a mtsikana – Kodi anali ndi udindo wotani? N'chifukwa chiyani anabwera kwa Yesu? Kodi anakumana ndi chotchinga chotani?<br>2. Yesu – Kukhudzidwa kwake ndi chilimbikitso.<br>3. Mtsikana – Vuto lake lalikulu, kumwalira ali ndi zaka khumi ndi ziwiri.<br>4. Anthu onyoza – Zinali zoyipa kwambiri kunyoza Ambuye Yesu. | Inu mupemphedwa kuti mulembe nkhani mu nyuzi, Nyuzi ya Galileya, yonena za mwana wamkazi wa Yairo amene waukitsidwa ndi mayi amene wachiritsidwa. Kambiranani awiriawiri ndi kudzafotokoza pa gulu kuti mukhale chiyani mu nkhaniyo. Onetsetsani kuti mwatsindika kuti Yesu atha kuukitsa munthu wakufa chifukwa Iye ndi Mulungu. ***(Aroma 1: 4)*** |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Pamene takhulupirira Ambuye Yesu, Iye amasintha miyoyo yathu kwamuyaya. Iye ali ndi mphamvu pa moyo ndi pa imfa. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Mu nthawi ya mavuto chitani zomwe anachita Yairo – kukhulupirira Ambuye Yesu ndi kudalira malonjezo amene anapereka m'Baibulo kwa amene ali ake. |

| | C3 – KALASI 3<br>Phunziro Lachitatu – Chodabwitsa cha chikhulupiriro<br>Mutu – Yesu athandiza wantchito wa msilikali | C3 – KALASI 4<br>Phunziro Lachitatu – Mphamvu ya Ambuye<br>Mutu – Kuthandiza osowa |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Luka 7: 1-10***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 7: 9***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu anakumana ndi kenturiyo amene wantchito wake ankadwala kwambiri.<br>2. Chikhulupiriro cha kenturiyo pa mawu ndi ntchito za Yesu ndi chitsanzo kwa aliyense. | **Werengani:** ***Mateyu 8: 1-13***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 8: 13***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu akuthandiza anthu ena awiri, onse awiri anaonetsa chikhulupiriro chachikulu mwa Iye.<br>2. Yesu akuonetsa chikondi chake pothandiza aliyense posatengera kuti ndi ndani. |
| MAWU OYAMBA | Fotokozani kumene nkhani yayambira. Aroma anali atatenga dziko lonse, kenturiyo (sanali Myuda) ndi munthu amene ankalamulira asilikali 100 ku malo ake ku Kapernao. Akuluakulu a Chiyuda anabwera kwa Yesu kudzamupempha kuti achiritse wantchito wa kenturiyo. Izi zinali zodabwitsa chifukwa iwo sankakhulupirira Yesu, koma anapemphedwa kuti apite kwa Yesu. | Funsani ana kuti atchule magulu osiyanasiyana a anthu amene amatsalidwa, kunyozedwa ndi kukanidwa pakati pa anzawo. Kumbutsani ophunzira kuti mu nthawi ya Yesu, anthu amene ankadwala matenda a khate komanso akapolo ankatsalidwa ndi kukanidwa. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Kenturiyo anamva za mphamvu yochiritsa ya Yesu. Iye ankachitira chifundo Ayuda ndipo anawamangira sunagoge, choncho akuluakulu a Chiyuda anamvera pempho lake ndipo anabwera kwa Yesu. ***(7: 1-4)***<br>2. Iwo anawuza Yesu kuti kenturiyo wa Amitundu uyu anali munthu wabwino, choncho Yesu ananyamuka kupita ku nyumba ya kenturiyo. ***(7: 5-6)***<br>3. Kenturiyo ankadziona kuti sanali woyenera kuti Yesu alowe m'nyumba mwake kapena kubwera kwa iye. Iye anatuma anzake kwa Yesu ndi uthenga. Koma, iye ankakhulupirira kuti Yesu angathe kuchiritsa wantchito wake ngakhale atapanda kubwera ku nyumba yake. Mawu okha ochokera kwa Iye angathe kuchiritsa wantchito wake. Kenturiyo anazindikira kuti monga iye anali pansi pa ulamuliro wa Boma la Chiroma ndipo asilikali ake anali pansi pa ulamuliro wake, Yesu analinso ndi ulamuliro omwewo pa matenda. ***(7: 6-8)***<br>4. Yesu anadabwa kwambiri ndi chikhulupiriro cha kenturiyo pakuti palibe ndi m'modzi yemwe wa Ayuda anavomereza kuti Yesu anali ndi ulamuliro wonse zimene iwo ankayenera kudziwa! ***(7: 9-10)***<br>5. *Pa **Marko 6: 6**, Yesu anadabwa ndi kusakhulupirira kwa Ayuda! Chikhulupiriro chachikulu cha kenturiyo chinalandira mphotho pamene wantchito wake anachiritsidwa. Chikhulupiriro chake mwa Yesu ndi chitsanzo cha aliyense.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Yesu athandiza wantchito wa msilikali. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Matenda a khate anali ochititsa mantha chifukwa panalibe mankhwala ochiritsa ndiponso wansembe ankamuchotsa m'nyumba mwake kuti azikakhala ndi anzake akhate mpaka atachira kapena kufa.<br>2. Munthu amene anali ndi khate anabwera kudzapempha Yesu kuti amuthandize.<br>3. Yesu anaonetsa chikondi pa wakhateyo potambasula dzanja lake ndi kumukhudza ndipo anachiritsidwa. Lamulo linkanena kuti wakhate akachiritsidwa azipita kwa wansembe kuti akamuone, motero Yesu anatumiza wakhateyo kwa wansembe kuti akatsimikize kuti khate lake lachoka ndi kuti atha kubwerera kwawo. ***(8: 1-4)***<br>4. Naye kenturiyo anabwera kwa Yesu kudzapempha thandizo la wantchito wake. Yesu analonjeza kupita ku nyumba yake. Kenturiyo anaonetsa ulemu ndi kudzichepetsa ponena kuti iye sanali woyenera kuti Yesu abwere ku nyumba yake.<br>5. Chikhulupiriro cha kenturiyo wa Chiroma, wa Amitundu, chikusonyeza kusiyana kwambiri ndi cha Ayuda. Mwachikondi chapadera ndi chifundo, akupempha Yesu kuti achiritse m'modzi mwa antchito ake. Iye ankakhulupirira kuti Yesu atha kuchiritsa ngakhale ali kutali. ***(8: 5-9)***<br>6. Chikhulupiriro cha kenturiyo chinadabwitsa Yesu – kunena zoona, chikhulupiriro cha Amitundu chinachititsa manyazi atsogoleri a Chiyuda a nthawi imeneyo. Chikhulupiriro cha kenturiyo chinali mphotho pamene wantchito wake anachiritsidwa nthawi yomweyo! ***(8: 10-13)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kuthandiza osowa. |
| KUKUMBUTSANA | Onaninso phunziro pokambirana izi:<br>• Kodi pempho la kenturiyo linali lotani?<br>• Kodi chinkavuta wantchito wake ndi chiyani?<br>• Kodi Yesu anachiona motani chikhulupiriro cha kenturiyo?<br>• Kodi Yesu anati chiyani za chikhulupiriro chimenechi?<br>• Kodi pa ***Ahebri 11: 6*** akuti tikuyenera kukhala ndi chiyani tisanayambe kukondweretsa Mulungu? | 1. Fanitsani nkhani ya kuchiritsidwa kwa wantchito wa kenturiyo mu nkhani iyi ndi pa ***Luka 7: 1-10***. Kambiranani za kusiyana ndi kufanana kwake.<br>2. Fananitsani mmene Yesu anachiritsira wakhate mu nkhani ino ndi kuyeretsa akhate pa ***Luka 17: 11-19***.<br>3. Kodi chakudabwitsa ndi chiyani pa nkhani imeneyi? |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Monga kenturiyo ankakhudzidwa mu mtima ndi wantchito wake, ifenso Akhristu tikuyenera kukhudzidwa mu mtima za kubweretsa ena kwa Yesu.<br>2. Muzikumbukira nthawi zonse kuti Ambuye Yesu ali ndi ulamuliro wonse pa dziko lapansi ndi Kumwamba posatengera zomwe ena amanena. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ndi kukhudza kwa Khristu kokha kumene kungachotse nthenda ya uchimo ndi kutipanga ife kukhala oyenera kupembedza Ambuye Yesu.<br>2. Ambuye Yesu anakondwera ndi chikhulupiriro cha kenturiyo. Ngati inu mukudalira Yesu, onetsetsani kuti cholinga chanu ndi kukondweretsa Ambuye Yesu. Ngati mutero, Iye adzakulemekezani ndi kukudalitsani. |

| | C3 – KALASI 3<br>Phunziro Lachinayi – Chodabwitsa cha chakudya<br>Mutu – Yesu athandiza anthu anjala | C3 – KALASI 4<br>Phunziro Lachinayi – Mphamvu ya Ambuye<br>Mutu – Kudyetsa anthu anjala |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Yohane 6: 1-15***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 6: 35***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu anaonetsa mphamvu yake podyetsa gulu lalikulu la anthu.<br>2. Yesu atha kukwaniritsa zosowa za onse amene angabwere kwa Iye ndi kumukhulupirira. | **Werengani:** ***Yohane 6: 1-15***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 6: 35***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Chodabwitsachi chinali chizindikiro mu Uthenga Wabwino wa Yohane chofuna kuonetsa kuti Yesu analidi Mwana wa Mulungu.<br>2. Titha kudalira Yesu kuti adzakwaniritsa zosowa za ku thupi ndi zauzimu za tsiku ndi tsiku. |
| MAWU OYAMBA | Werengani mavesi asanu ndi limodzi oyambirira a Ndime Yowerenga. Kenaka yerekezani mmene zinalili, za vuto lodyetsa gulu lalikulu kwambiri la anthu ku malo kopanda kanthu. Ganizirani za vuto lomwe ophunzira anali nalo pamene Yesu anawawuza kuti apeze chakudya cha gulu la anthuwo. | Chodabwitsa ichi ndi chapadera chifukwa ndi chokhachi chimene chinalembedwa m'Mauthenga onse Abwino. Ndi chodabwitsa chokhachi chimene anthu ochuluka nthawi imodzi akulandira madalitso. Kumbutsani ophunzira kuti Yesu amakonda aliyense ndipo akufuna kuti aliyense akhulupirire ndi kutsatira Iye. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Pamene Ambuye Yesu anaona gulu lalikulu la anthu nthawi imeneyi, maganizo ake oyamba anali ofuna kuwapatsa chakudya. Iye anafunsa Filipo komwe akanatha kukagula buledi, koma Filipo anaganiza za ndalama osati za kuti Yesu anali ndi mphamvu zodyetsa aliyense. ***(6: 1-7)***<br>2. Ngakhale Andreya ankaganizanso kuti kunali kovuta kudyetsa gulu la anthu lotere, iye anafotokoza za mnyamata amene anali ndi buledi msanu ndi nsomba ziwiri. Ngakhale analibe zokwanira, mnyamatayu anapereka zonse kwa Yesu. ***(6: 8-9)***<br>3. Yesu atayamika, anapereka chakudyachi kwa ophunzira ake kuti agawe. Anthu anadya zonse zimene ankafuna ndipo Yesu anawuza ophunzira ake kuti atole zotsala kufuna kutiphunzitsa kuti tisamaononge zinthu zimene Iye amatipatsa tsiku ndi tsiku. ***(6: 10-13)***<br>4. *Yesu anagwiritsa ntchito chodabwitsa ichi kufotokoza kuti "Iye ndi mkate wamoyo" amene amatipatsa moyo wosatha kuti tikhale okhutitsidwa kuuzimu. (onani Vesi Yoloweza)*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Yesu athandiza anthu anjala. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yesu anachoka ku Yerusalemu ndi kupita kumpoto kwa Nyanja ya Galileya ndipo gulu lalikulu la anthu linamutsatira chifuka anaona zodabwitsa anazichita. Gulu la anthu linali ngati 'nkhosa zopanda m'busa' ***(Marko 6: 34)*** ndipo Yesu anamva nawo chisoni.<br>2. Chikhulupiriro cha ophunzira zinali chochepa pa nkhani ya kudyetsa gulu la anthu. Filipo anaganiza za ndalama osati zakuti Yesu anali ndi mphamvu ya kudyetsa aliyense. Andreya anaona mnyamata amene anali buledi msanu ndi nsomba ziwiri koma ankakayikira ngati zikanakhala zothandiza. ***(6: 1-9)***<br>3. Yesu analamulira kuti anthu onse akhale pansi. Atayamika, Iye anachulukitsa buledi ndi nsomba, ndipo anazipereka kwa ophunzira kuti agawire anthuwo. ***(6: 10-11)***<br>4. Panalibe amene chinamuperewera ndipo anawuzidwa kuti anthu onse anakhuta. Tikuwuzidwa kuti Ambuye Yesu analamula ophunzira ake kuti atole zakudya zotsala! Chodabwitsa chachikulu chinachitika! ***(6: 12-13)***<br>5. Gulu la anthu linazindikira kuti chinali chodabwitsa ndipo anavomereza kuti Yesu anali mneneri amene analosera pa ***Deuteronomo 18: 15***. Koma, chikhulupiriro chawo sichinali chenicheni, iwo sanali okonzeka kuvomereza kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu kapenanso kulapa machimo awo ndi kumulandira kukhala Mpulumutsi wawo.<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Kudyetsa anthu anjala. |
| KUKUMBUTSANA | Onaninso phunziro pofuna ana kuti ayerekeze kuti nkhaniyi akuyilemba mu nyuzi. Kodi mtolankhani angalembe zotani za:<br>(i) Zomwe gululi linkaonekera?<br>(ii) Chifundo cha Ambuye Yesu?<br>(iii) Mafunso a ophunzira?<br>(iv) Zomwe Ambuye Yesu anapereka?<br>(v) Maganizo a Ambuye Yesu pa za kutaya chakudya? | Gawani Zowerenga izi m'magulu atatu.<br>***Mateyu 14: 13-21, Marko 6: 33-44, Luka 9: 10-17***<br><br>Kambiranani zomwe gulu lililonse laphunzira za nkhaniyi m'magulu awo zimene mulibe mu Uthenga Wabwino wa Yohane. Magulu onse atatu afotokoze ndi kugawana ndi anzawo zonse zimene apeza. |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Vesi Yoloweza ikutiwuza kuti tikuyenera kubwera kwa Yesu amene ndi Mkate Wamoyo, amene adzakwaniritsa chosowa cha mu mtima mwathu.<br>2. Yesu akufuna achinyamata kuti azimutumikira. Monga anachitira mnyamata uyu. Chomwe anapereka chinathandiza Yesu kuchita chodabwitsa chapamwamba. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Ngati inu mukudalira Yesu, Iye adzakupatsa chakudya chanu cha thupi ndi cha uzimu.<br>2. Monga Yesu anachulukitsa buledi msanu ndi nsomba ziwiri, Iye atha kugwiritsa ntchito ndi kuchulukitsa chilichonse chimene tingamupatse ngati ndife anthu ake. Izi zitha kukhala maluso athu, nthawi yathu kapena ndalama zathu. Ngati timupatsa Iye, Iye adzatipatsa mphotho. |

<table>
<tr><th></th><th>C4 – KALASI 3<br>Phunziro Loyamba – Imfa ya Khristu<br>Mutu – Mpsopsono wa womupereka</th><th>C4 – KALASI 4<br>Phunziro Loyamba – Ambuye Yesu<br>Mutu – Kuweruzidwa ndi kupachikidwa</th></tr>
<tr><td></td><td>Werengani: Mateyu 26: 36-56<br>Vesi Yoloweza: Mateyu 26: 39<br><br>Ife tikuphunzira kuti:<br>1. Yesu anapemphera m'Munda wa Getsemane ndipo anaperekedwa ndi Yudase kwa olamulira.<br>2. Kufunika kwa pemphero mu nthawi ya zovuta.</td><td>Werengani: Luka 23: 1-33<br>Vesi Yoloweza: Aroma 5: 8<br><br>Ife tikuphunzira kuti:<br>1. Yesu anaweruzidwa kuti akaphedwe ngakhale anali wosalakwa.<br>2. Chinali chikonzero cha Mulungu cha chipulumutso kuti Yesu apachikidwe pa mtanda chifukwa cha machimo athu.</td></tr>
<tr><td>MAWU OYAMBA</td><td>Funsani ana akuwuzeni zinthu zimene zinawachitikira zomwe zinapangitsa kuti amadandaula, kukhala ndi nkhawa kapena kuchita nazo mantha.<br>Kodi iwo akuyenera kuchita chiyani kuti zinthu zikhale bwino m'miyoyo yawo?</td><td>Funsani ana ngati wina anawanenera zinthu zimene iwo sanachite. Afunseni kuti alembe zomwe iwo ankamva mu mtima mwawo pa zimene zinkawachitikira.</td></tr>
<tr><td>KUTSIRIZA</td><td>Perekani Nkhani ya m'Baibulo<br><br>Kambiranani ndi Kufotokoza:<br>1. Yesu ndi ophunzira ake anapita ku Munda wa Getsemane. Iye anawapempha kuti azipemphera. Iye ankadziwa zomwe zidzamuchitikire, zomwe zinamuchititsa kumva chisoni kwambiri. (26: 36-38)<br>2. M'pemphero lake, Yesu anati anali wofuna kuchita chilichonse chimene Atate ake ankafuna kuti Iye achite. Maganizo a mazunzo amene adzadutsamo zinamumvetsa chisoni. (26: 39)<br>3. Yesu anabwera kwa ophunzira ake katatu ndipo nthawi iliyonse ankawapeza akugona. (26: 40-44)<br>4. Kenaka wophunzira wa Yesu, Yudase, anabwera kudzamupereka kwa asilikali. (26: 47-49)<br>5. Yesu akanatha kuthawa koma anapita ndi asilikaliwo mwa kufuna kwake chifukwa ankadziwa kuti ichi chinali chifuniro cha Atate. (26: 47-56)<br>6. Kambiranani za kufunika koti Ambuye Yesu amvere chifuniro cha Atate ake ndi kupita pa mtanda kuti anthu apulumutsidwe.<br><br>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.<br>Tsirizani Phunziro Loyamba.<br><br>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Mpsopsono wa womupereka.</td><td>Perekani Nkhani ya m'Baibulo<br><br>Kambiranani ndi Kufotokoza:<br>1. Yesu anaweruzidwa ndi bwanamkubwa wa Chiroma, Pilato. Iye ankazengedwa mlandu woletsa anthu kupereka msonkho kwa Kaisara ndi kunena kuti anali Khristu Mfumu. Pilato analengeza kuti Yesu anali wosalakwa. (23: 1-4)<br>2. Pilato atazindikira kuti Yesu anali wochokera ku Galileya, anamutumiza kwa Herode amene ankalamulira dera limenelo. Mfumu Herode anamuseka ndi kumunyoza Yesu kenaka anamutumizanso kwa Pilato chifukwa sanapeze cholakwa chilichonse. (23: 6-15)<br>3. Pilato anali ndi wam'ndende wina amene anapha munthu. Nthawi imeneyi pa chaka, iye ankamasula wam'ndende m'modzi ndipo anafuna kumasula Yesu. Anthu anakakamiza Pilato kuti awamasulire Baraba ndi kupachika Yesu. (23: 18-23)<br>4. Pilato analibe mphamvu zoti akanatha kuletsa anthuwo, motero anawalola kuti atenge Yesu kuti amupachike. (23: 24-25)<br><br>Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.<br>Tsirizani Phunziro Loyamba.<br><br>Kuonetsa: Onani FBI pa Zoonjezera B – Kuweruzidwa ndi kupachikidwa.</td></tr>
<tr><td>KUKUMBUTSANA</td><td>Lembani ziganizo zisanu ndi ziwiri izi, chilichonse pa pepala lake. Sakanizani mapepalawo ndipo ana ayike mu ndondomeko ya momwe zinachitikira.<br>1. Yesu anapita ku Getsemane ndi ophunzira ake.<br>2. Yesu anatenga ophunzira atatu ndi kupita nawo kukapemphera.<br>3. Ophunzira atatuwo anagona tulo.<br>4. Yudase anafika ndi gulu lalikulu.<br>5. Yudase anapsopsona Yesu.<br>6. Asilikali anagwira Yesu.<br>7. Ophunzira onse anathawa.</td><td>Kuweruzidwa kwa Yesu kunali kosatsatira malamulo. Funsani ophunzira kuti aganizire kuti ndi zinthu zingati zomwe zinachitika kwa Yesu mu nkhaniyi zomwe zinali zosakhala bwino ndi zophwanya malamulo.</td></tr>
<tr><td>KHALANI MOYO UMENEWU</td><td>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:<br>Kodi ndi njira ziti zomwe Akhristu 'amapereka' Ambuye Yesu lero?<br>Kambiranani zomwe angachite kuti izi zisamachitike.</td><td>Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:<br>Kodi ine ndinamuyamika Yesu chifukwa cha kufera machimo anga pa mtanda? (Vesi Yoloweza)<br>Kodi ndimakhala mbali ya Yesu pamene anthu pa dziko lapansi akudana naye ndi kunyoza amene amutsatira?</td></tr>
</table>

| | C4 – KALASI 3<br>**Phunziro Lachiwiri – Imfa ya Khristu**<br>**Mutu – Chisankho cha bwanamkubwa** | C4 – KALASI 4<br>**Phunziro Lachiwiri – Ambuye Yesu**<br>**Mutu – Kuyikidwa m'manda ndi kuuka** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Mateyu 27: 1, 2, 11-31***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 27: 22***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Pilato, bwanamkubwa wa Chiroma, ankadziwa kuti Yesu anali wosalakwa, koma chifukwa chokakamizidwa Pilato anamasula chigawenga ndi kupereka Yesu kuti akapachikidwe.<br>2. Chinali chikonzero cha Mulungu cha chipulumutso kuti Yesu apachikidwe pa mtanda chifukwa cha machimo athu. | **Werengani:** ***Luka 23: 44-56 ndi 24: 1-12***<br>**Vesi Yoloweza:** ***2 Timoteo 2: 8***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu atafa, Yosefe anatenga thupi lake ndi kukaliyika m'manda atsopano.<br>2. Panapita masiku ochepa, monga mmene Yesu ananenera kwa ophunzira ake, m'manda muli mopanda kanthu ndipo Yesu anali atauka kwa akufa! |
| MAWU OYAMBA | Funsani ophunzira kuti afotokozere anzawo zisankho zomwe achita posachedwapa. Afunseni kuti alembe zisankho zabwino ndi zoyipa. Kodi kunali kosavuta kapena kovuta kuti achite chisankho chimenecho? | Funsani ophunzira kuti afotokoze za nkhani zachisoni kapena zoyipa zomwe zinawachitikira. Afunseni kuti afananitse zimenezo ndi nthawi za chisangalalo m'miyoyo yawo. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Atagwira Yesu, iwo anapita naye kwa bwanamkubwa wa Chiroma, Pilato. Yesu sanayankhe mafunso onse a Pilato. Pilato atsimikiza kuti Yesu sanalakwe chilichonse. ***(27: 11-14)***<br>2. Pilato anali ndi wam'ndende wina wotchedwa Baraba, amene anayambitsa ziwawa ndi kupha munthu. Pa nthawi imeneyi pa chaka, iye ankamasula wam'ndende m'modzi motero iye ankafuna kumasula Yesu. Anthu anakakamiza Pilato kuti amasule Baraba ndipo alole kuti Yesu apachikidwe. ***(27: 15-23)***<br>3. Pilato anaona kuti zinthu zikuvuta ndipo kukhala ziwawa ngati samupereka Yesu. Choncho Pilato anagonjera zofuna za anthu ndipo analola kuti atenge Yesu ndi kukamupachika, kenaka anamasula Baraba ***(27: 24- 26)***<br>4. *Tonse timachita chisankho cha zomwe tidzachita ndi Ambuye Yesu. Titha kumulandira kukhala Ambuye ndi Mpulumutsi kapena kukana kumulandira m'mitima mwathu ndi m'miyoyo yathu.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Chisankho cha bwanamkubwa. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yesu atafa lachisanu masana, munthu wina wotchedwa Yosefe, wochokera ku mudzi wa Arimateya anapeza chilolezo choti atsitse thupi la Yesu ndi kulaliyika m'manda. Iye anagubuduza mwala waukulu kutseka pa khomo la mandawo. ***(23: 50-53)***<br>2. M'mawa tsiku lamulungu, amayi ena anabwera atanyamula zonunkhiritsa kuti adzoze thupi la Yesu. Iwo anapeza kuti mwala uja wachotsedwa ndipo m'manda munalibe thupi la Yesu. ***(24: 1-3)***<br>3. Angelo awiri anaoneka ndipo anawuza amayiwo kuti Yesu ali ndi moyo. ***(24: 4-8)***<br>4. Amayi anathamanga kupita kukawuza ophunzira aja. Ophunzira anadabwa kwambiri ndipo sanakhulupirire amayiwo. ***(24: 9-11)***<br>5. Petro anathamanga kupita ku manda koma anachokako akudabwa ndi zomwe zinachitikazo. ***(24: 12)***<br>6. *Gwiritsani ntchito* ***1 Akorinto 15: 3-4*** *kuti mulembe za kufunika kwake kwa zochitika nthawi imeneyi.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kuyikidwa m'manda ndi kuuka! |
| KUKUMBUTSANA | Funsani alembe zosiyana zambiri za pakati pa Yesu ndi Baraba. | Kuchokera pa Ndime Yowerenga mu phunziro lino, kambiranani zomwe anachita anthu osiyana awa a) Mkulu wa asilikali a Chiroma, b) gulu la anthu, c) amayi m'mawa wa lamulungu, d) ophunzira, ndi e) Petro. |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Pilato analola kuti achite zomwe gulu la anthu linkafuna. Ifenso, tikuyenera kusamala kuti anthu ena asatisocheretse pochita ziganizo zolakwika! | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Werengani ***Aroma 10: 9*** ndi kuona zotsatira zake pa aliyense. |

| | C4 – KALASI 3<br>**Phunziro Lachitatu – Imfa ya Khristu**<br>**Mutu – Manda a munthu wachuma** | C4 – KALASI 4<br>**Phunziro Lachitatu – Ambuye Yesu**<br>**Mutu – Kumuona ndi kumva** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Marko 15: 37, 42-47 ndi Marko 16: 1-8***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Akorinto 15: 3-4***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu atafa, Yosefe anatenga thupi lake ndi kukaliyika m'manda atsopano.<br>2. Patapita masiku ochepa, monga mmene Yesu ananenera kwa ophunzira ake, m'manda munali mopanda kanthu, ndipo Yesu anali atauka kwa akufa! | **Werengani:** ***Luka 24: 13-35***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 24: 26***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Tsiku lomwelo limene Yesu anauka kwa akufa, Iye anabwera ndi kuyenda ndi omutsatira ake awiri amene ankapita ku Emau.<br>2. Monga anthu ambiri, iwo anasokonezeka maganizo chifukwa cha zonse zimene zinachitika ndipo sankamvetsa kuti Yesu anali moyo. |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ophunzira kuti afotokoze za nkhani zachisoni kapena zoyipa zomwe zinawachitikira. Afunseni kuti asiyanitse zimenezo ndi nthawi za chisangalalo m'miyoyo yawo. | Funsani ana za kutalika kwa ulendo umene iwo anayenda tsiku limodzi. Kodi iwo ankakambirana chiyani mmene ankayenda? Mu nkhani iyi anthu awiri anayenda mtunda wa makilomita khumi ndi imodzi kupita ndi kubwera tsiku lomwelo. Thandizani ana kuti amvetse za kutalika kwake. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Yesu atafa lachisanu masana, munthu wina wotchedwa Yosefe wochokera ku mudzi wa Arimateyu anapeza chilolezo choti atsitse thupi la Yesu ndi kulaliyika m'manda. Iye anagubuduza mwala waukulu kutseka pa khomo la mandawo. ***(15: 42-47)***<br>2. M'mawa tsiku lamulungu, amayi ena anabwera atanyamula zonunkhiritsa kuti adzoze thupi la Yesu. Iwo anapeza kuti mwala uja wachotsedwa ndipo m'manda munalibe thupi la Yesu. ***(16: 1-5)***<br>3. Mngelo anaonekera ndipo anawuza amayiwo kuti Yesu anali ndi moyo. ***(16: 6)***<br>4. Mngelo analangiza amayiwo kuti akuwuze ophunzira zimene zachitikazo. Amayiwo anachita mantha kwambiri, choncho anathamanga ndipo sanawuze wina aliyense. ***(16: 7-8)***<br>5. *Gwiritsani ntchito* ***1 Akorinto 15: 3-4*** *(Mavesi Oloweza) kuti mufotokoze za kufunika kwake kwa zochitika nthawi imeneyi.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Manda a munthu wachuma. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Otsatira Yesu awiri ankayenda kuchokera ku Yerusalemu kupita ku Emau. Iwo anasokonezeka m'maganizo chifukwa cha zimene zinachitika. ***(24: 13-15)***<br>2. Panabwera munthu wina kumayenda nawo koma sankamuzindikira kuti anali Yesu. Iwo ankaganiza kuti anali mlendo. Iwo anafotokoza kuti anali achisoni chifukwa cha imfa ya Yesu. ***(24: 18-24)***<br>3. Pamene iwo ankayenda, Yesu anafotokoza kuti aneneri a Chipangano Chakale analosera zonse zimene zinachitika mu Yerusalemu. ***(24: 25-27)***<br>4. Popeza kunali kukuda, ophunzira aja anapempha Yesu kuti apite ku nyumba yawo kuti agone usiku umenewo. Pamene ankadya, mwadzidzidzi iwo anazindikira kuti munthu wachilendo uja anali Yesu; nthawi yomweyo anasowa pakati pawo! ***(24: 28-31)***<br>5. Ophunzira awiriwa anabwerera mofulumira ku Yerusalemu usiku omwewo kukawuza ena zomwe zinawachitikira komanso kukafotokoza nkhani yabwino ya kuti Yesu anali moyo. ***(24: 33-35)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kumuona ndi kumva. |
| **KUKUMBUTSANA** | • Kodi mu nkhani imeneyi muli umboni wotani wosonyeza kuti Yesu anafadi?<br>• Kodi mu nkhani imeneyi muli umboni wotani wosonyeza kuti Yesu anaukadi?<br>• Kodi mungamutsimikizire motani munthu amene akukayika kuti zimenezi ndi zoona? | • Kodi anthu awiri a pa ulendowa ankamva bwanji mu mtima mwawo koyambirira kwa nkhaniyi?<br>• Kodi anamva bwanji mu mtima mwawo kumapeto kwa nkhaniyi?<br>• Kodi mukuganiza kuti ndi chiyani chomwe chinasintha zinthu?<br>• Fufuzani maulosi ena amene Yesu anayankhula osonyeza kuti ankayenera kufa! |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Ngati ndakhulupirira Ambuye Yesu kukhala Mpulumutsi wanga, ine ndiyenera kufunitsitsa kupita kukawuza ena za Iye, makamaka zakuti Iye ali ndi MOYO! | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Ngati ndakhulupirira Ambuye Yesu kukhala Mpulumutsi wanga, ine ndiyenera kufunitsitsa kupita kukawuza ena za Iye, makamaka zakuti Iye ali ndi MOYO! |

| | **C4 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachinayi – Imfa ya Khristu**<br>**Mutu – Mawu a mlendo** | **C4 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachinayi – Ambuye Yesu**<br>**Mutu – Kukayikira ndi kukhulupirira** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Luka 24: 13-35***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 24: 26***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Pa tsiku lomwe Yesu anauka kwa akufa, anayenda pamodzi ndi omutsatira ake awiri kupita ku Emau.<br>2. Monga anthu ambiri, iwo anasokonezeka maganizo chifukwa cha zonse zimene zinachitika ndipo sankamvetsa kuti Yesu anali moyo. | **Werengani:** ***Yohane 20: 19-31***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Yohane 20: 29***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Yesu atauka kwa akufa, anaonekera kwa ophunzira ake. Tomasi panalibe ndipo sanakhulupirire kuti iwo anaonadi Yesu.<br>2. Ife sitinaone Ambuye Yesu Woukitsidwayo, koma Yesu anati “Ndi odala amene amakhulupirira ngakhale asanaone.” |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ana za kutalika kwa ulendo umene iwo anayenda tsiku limodzi. Kodi iwo ankakambirana chiyani mmene ankayenda? Mu nkhani iyi anthu awiri anayenda mtunda wa makilomita khumi ndi imodzi kupita ndi kubwera tsiku lomwelo. Thandizani ana kuti amvetse za kutalika kwake. | Kodi mnzanu anakuwuzanipo nkhani yoona imene kwa inu inali yovuta kukhulupirira? Funsani ophunzira ena apereke zitsanzo za nkhani ngati zimenezo. Kodi iwo anamva bwanji mu mtima mwawo pamene anazindikira kuti zinali zoona? |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Otsatira Yesu awiri ankayenda kuchokera ku Yerusalemu kupita ku Emau. Iwo anasokonezeka m’maganizo chifukwa cha zimene zinachitika. ***(24: 13-15)***<br>2. Panabwera munthu wina kumayenda nawo koma sankamuzindikira kuti anali Yesu. Iwo ankaganiza kuti anali mlendo. Iwo anafotokoza kuti anali achisoni chifukwa cha imfa ya Yesu. ***(24: 18-24)***<br>3. Pamene iwo ankayenda, Yesu anafotokoza kuti aneneri a Chipangano Chakale analosera zonse zimene zinachitika mu Yerusalemu. ***(24: 25-27)***<br>4. Popeza kunali kukuda, ophunzira aja anapempha Yesu kuti apite ku nyumba yawo kuti agone usiku umenewo. Pamene ankadya, mwadzidzidzi iwo anazindikira kuti munthu wachilendo uja anali Yesu; nthawi yomweyo anasowa pakati pawo! ***(24: 28-31)***<br>5. Ophunzira awiriwa anabwerera mofulumira ku Yerusalemu usiku omwewo kukawuza ena zomwe zinawachitikira komanso kukafotokoza nkhani yabwino ya kuti Yesu anali moyo. ***(24: 33-35)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Mawu a mlendo. | **Perekani Nkhani ya m’Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Ngakhale anamva kuti Yesu wauka, ophunzira anadzitsekera m’nyumba chifukwa ankaopa atsogoleri a Chiyuda. ***(20: 19)***<br>2. Usiku omwewo, mwadzidzidzi Yesu anaonekera m’nyumbamo makomo ali chitsekere. Iye anawaonetsa mabala a kukhomedwa kwake pa mtanda. Izi zinawatsimikizira kuti Iye analidi moyo, ndipo zinawapatsa chimwemwe chachikulu. ***(20: 20)***<br>3. M’modzi mwa ophunzira, wotchedwa Tomasi, panalibe usiku umenewo ndipo sanakhulupirire pamene ena aja anamuwuza kuti anaona Yesu. Iye ankafuna kukhala ndi umboni asanakhulupirire. ***(20: 24-25)***<br>4. Patatha sabata imodzi, ophunzira onse, kuphatikiza Tomasi, anali pamodzi. Yesu anaonekera monga anachitira poyamba paja. Iye anaonetsa Tomasi manja ndi mapazi ake, motero Tomasi anazindikira kuti analidi Yesu. ***(20: 26-27)***<br>5. Tsopano Tomasi anali ndi chitsimikizo kuti Yesu anali moyo ndipo iye ananena kwa Iye kuti, “Ambuye wanga ndi Mulungu wanga.” ***(20: 28)***<br>6. *Tomasi nthawi zambiri amatchedwa “Tomasi Wokayikira” chifukwa sanakhulupirire mpaka ataona Yesu ali moyo. Lero ife sitimuona Iye koma timakhulupirira kuti ali moyo ndi kuti tsopano ali Kumwamba.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Kukayikira ndi kukhulupirira. |
| **KUKUMBUTSANA** | • Kodi anthu awiri a pa ulendowa ankamva bwanji mu mtima mwawo koyambirira kwa nkhaniyi?<br>• Kodi anamva bwanji mu mtima mwawo kumapeto kwa nkhaniyi?<br>• Kodi mukuganiza kuti ndi chiyani chomwe chinasintha zinthu?<br>• Fufuzani maulosi ena amene Yesu anayankhula osonyeza kuti ankayenera kufa. | • Kodi chinali chiyani chimene chinatsimikizira ophunzira aja kuti aonadi Yesu?<br>• Kodi ndi chiyani chinachititsa Tomasi kuzindikira kuti analakwitsa?<br>• Kodi Vesi Yoloweza ikutikhudza motani lero?<br>• Onani pa ***Yohane 20: 30-31*** ndi kukambirana chifukwa chimene Yohane analembera Uthenga wake. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>Ophunzira anasangalala kwambiri pamene anazindikira kuti Yesu anali moyo! Iye anadzionetsera yekha kuti analidi Mwana wa Mulungu. Iwo ankafuna kuwuza ena za nkhani yabwino imeneyi. Kodi izi zikuyenera kukhudza motani miyoyo yathu lero? | **Zomwe tikuphunzira m’phunziroli:**<br>Anthu ena lero amakayika za kuti Yesu ali ndi moyo chifukwa sanamuone. Kodi ***Yohane 20: 29*** akutsimikizira motani amene amakhulupirira? |

## C5 – KALASI 3
**Phunziro Loyamba – Rute**
**Mutu – Zisankho zolakwika**

**Werengani:** ***Rute 1: 1-14***
**Vesi Yoloweza:** ***Oweruza 21: 25***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Nkhani ya m'buku la Rute Chaputala 1 ikukhudza zisankho za anthu.
2. Nthawi zina tonse timayenera kuchita zisankho zofunika. Tikuyenera kuchita zisankho motsogozedwa ndi Mulungu. Zisankho zathu zitha kukhudza ena.

### MAWU OYAMBA

M'magulu kapena anthu awiriawiri funsani ana kuti akambirane izi:
- Zifukwa zomwe anthu amachoka ndi kupita ku malo atsopano kapena dziko latsopano.
- Zovuta zimene amakumana nazo pamene akufuna kukhala ku malo atsopano.

Mutha kungolemba maganizo anu kapenanso kuwaonetsa monga ngati ulusi wa 'kangaude'.
M'njira ina, ngati anapita ku dera latsopano, iwo akonzekera kugawana ndi anzawo zomwe zinawachitikira.

### KUTSIRIZA

**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Aisrayeli anali atachoka pamaso pa Mulungu; aliyense ankangochita zinthu zomukomera yekha. **(Vesi Yoloweza)**
2. Pamene nkhani ikupitirira, anthu akuchita zisankho zofunika, zina zabwino kuposa za ena. Elimeleki, Naomi ndi ana awo aamuna, Maloni ndi Kilioni ankakhala ku Betelehemu kutanthauza 'Nyumba ya Chakudya', koma njala inafika m'dzikomo. Elimeleki anaganiza zotenga banja lake kupita ku Moabu, dziko limene anthu ake ankapembedza mafano. Ife sitikuwuzidwa kuti anapemphera. *Kodi iye akanakhulupirira Mulungu kuti adzawaptasa chakudya m'dziko lawo lomwelo?* ***(1: 1-2)***
3. Ku Moabu zovuta zinawagwera; Elimeleki anamwalira. Maloni ndi Kilioni anakwatira atsikana a Chimoabu, Rute ndi Oripa, koma Maloni ndi Kilioni anamwaliranso. ***(1: 3-5)***
4. Naomi atamva kuti njala yatha, anafuna kubwerera ku Betelehemu. Apongozi ake awiriwo anafunanso kupita naye. Iye anayamikira chifundo chawo koma anawapempha kuti abwerere ku mabanja awo. Pamapeto pake Oripa anabwerera koma Rute anachita chisankho chopita ndi Naomi. ***(1: 6-14)***
5. *Fotokozani chifukwa chomwe Naomi ankafunira kuti atsikanawo abwerere kwawo, ndi chifukwa chimene Oripa anabwerera kwawo ku Moabu. Ganizirani za nkhawa za Rute pochita chisankho chopita ku dziko lachilendo. Fotokozani chifukwa chomwe Naomi ankafunira kuti atsikanawo abwerere komanso chifukwa chimene chinachititsa Oripa abwerere ku Moabu.*

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Loyamba.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Zisankho zolakwika.

### KUKUMBUTSANA

Funsani ana kuti alembe zisankho zina zimene iwo adzayenera kuchita sabata ya mawa, komanso nthawi ina pa moyo wawo. Gwiritsani ntchito manambala kuyamba ndi chofunika kwambiri (1 = chofunika kwambiri, ndi zina).

### KHALANI MOYO UMENEWU

**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Kambiranani momwe zisankho zimene timachita zimakhala ndi zotsatira zake - kwa ife eni ndi kwa ena. Chisankho cha Elimeleki chinabweretsa banja lake pakati pa chikhalidwe chimene sichinkadziwa Mulungu. Chisankho cha Naomi chobwerera kwawo chinkatanthauza kuti naye Rute ndi Oripa ankayenera kuchitanso zisankho.
2. Tingathe kupeza thandizo kwa Mulungu pamene tikuchita zisankho. (Kupemphera, kuwerenga Baibulo, kufunsa nzeru kwa Akhristu achikulire)
3. Chisankho chofunika kwambiri pa moyo wathu ndi chimene timachita tikamva za Ambuye Yesu Khristu.

## C5 – KALASI 4
**Phunziro Loyamba – Rute**
**Mutu – Banja lochoka pamaso pa Mulungu**

**Werengani:** ***Rute 1: 1-14***
**Vesi Yoloweza:** ***Oweruza 21: 25***

**Ife tikuphunzira kuti:**
1. Nkhani ya m'buku la Rute ikukhudza zisankho za anthu.
2. Nthawi zina tonse timayenera kuchita zisankho zofunika. Tikuyenera kuchita zisankho motsogozedwa ndi Mulungu. Zisankho zathu zitha kukhudza ena.

### MAWU OYAMBA

Kodi zisankho ndi zofunika motani? Perekani zitsanzo za zisankho ndipo funsani ana aunike kufunika kwake pokweza kadi - X (chosafunika), ~ (chofunika pang'ono), ! (chofunika kwambiri).
Zitsanzo: Choti tidye masana, kugona kapena kupita ku tchalichi, mtundu wa zovala zoti mugule, kukhulupirira Yesu kukhala Mpulumutsi wanu, mitu yoti uphunzire, kukafotokoza za kuzunzana pa sukulu kapena ayi ndi zina zambiri.

### KUTSIRIZA

**Perekani Nkhani ya m'Baibulo**

**Kambiranani ndi Kufotokoza:**
1. Mmene zinkachitikira: Mu nthawi ya Oweruza, kunalibe atsogoleri owopa Mulungu; aliyense ankachita zomukomera yekha. **(Vesi Yoloweza)**
2. Ichi ndiye chinali chifukwa cha njala mu Israyeli ngakhale Mulungu analonjeza kuti linali dziko "loyenda mkaka ndi uchi." ***(Deuteronomo 30: 15-20)***
3. Elimeleki anasankha zotenga banja lake ndi kupita ku Moabu, dziko lopembedza mafano. Anayika Mulungu kumbali pa chikonzero chawo. ***(1: 1-2)***
4. Mavuto anabwera kawiri; Elimeleki anamwalira kusiya Naomi wamasiye. Ana ake Maloni ndi Kilioni, atakwatira atsikana a Chimoabu, Rute ndi Oripa, anamwaliranso ndipo analibe ana. ***(1: 3-5)***
5. Naomi anaganiza zobwerera kwawo chifukwa tsopano kunali chakudya ku Betelehemu. Naomi anali ndi udindo wosamalira apongozi akewo. Iye anawayamikira chifukwa cha chifundo chawo koma iye anazindikira kuti sakanathanso kuwapatsa amuna ena atsopano. Naomi anawapempha kuti abwerere ku mabanja awo.
6. Aliyense anachita chisankho pa yekha: Oripa anabwerera kwawo; Rute anapita ndi Naomi. ***(1: 6-18)***
7. *Fotokozani chifukwa chomwe Naomi ankafunira kuti atsikanawo abwerere kwawo, ndi chifukwa chimene Oripa anabwerera kwawo ku Moabu. Ganizirani za nkhawa za Rute pochita chisankho chopita ku dziko lachilendo.*

**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**
**Tsirizani Phunziro Loyamba.**

**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Banja lochoka pamaso pa Mulungu.

### KUKUMBUTSANA

Awiriawiri, ganizirani zokambirana za Rute ndi Oripa kuti zinali zotani pamene ankayankhulana za ubwino ndi kuyipa kopita ku Betelehemu ndi Naomi kapenanso kubwerera ku mabanja awo ku Moabu.

### KHALANI MOYO UMENEWU

**Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**
1. Zisankho zimene timachita zimakhala ndi zotsatira zake - kwa ife eni ndi kwa ena. Ganizirani za chisankho cha ntchito yathu, abwenzi, kukwatira, kugwiritsa ntchito ndalama kapena nthawi yanu ndi zina zambiri.
2. Werengani ***Miyambo 3: 5-6 ndi 14: 12***. Tidzachita chisankho chabwino ngati Mulungu adzatithandiza. Kodi tingachite izi motani?

| | **C5 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachiwiri – Rute**<br>**Mutu – Kubwerera kwa akazi amasiye** | **C5 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachiwiri – Rute**<br>**Mutu – Naomi abwerera kwa Mulungu** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Rute 1: 14-22 ndi 2: 1-3***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Rute 1: 16-17***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kukonda Naomi ndi chikhulupiriro mwa Mulungu wa Naomi zinathandiza Rute kulimba mtima kupita ndi kukakhala ku dziko latsopano.<br>2. Aliyense wa ife akuyenera kusankha kukhulupirira Mulungu kapena kukhala ndi zinthu zina zofunika pa miyoyo yathu. | **Werengani:** ***Rute 1: 15-22***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Rute 1: 16-17***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Kukonda Naomi ndi chikhulupiriro mwa Mulungu wa Naomi zinathandiza Rute kulimba mtima kupita ndi kukakhala ku dziko latsopano.<br>2. Chikhulupiriro mwa Mulungu ndi kudzipereka kwa Iye, zimatithandiza kuchita zisankho zovuta, kuchita zomwe sitikudziwa zotsatira zake.<br>3. Kukhulupirika m'banja, kwa anzathu ndi kudzipereka kwa Ambuye Yesu ndiye zimakondweretsa Mulungu. |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ana atchule munthu wamkulu amene amachita naye chidwi. Afunseni alembe zifukwa zisanu zomwe zimawachitsa chidwi pa munthu ameneyo. Afotokozere gulu lonse zifukwa zina.<br>Mu nkhani iyi, Rute anadzipereka kwa apongozi ake. Kodi mwina ndi makhalidwe amene anaona mwa Naomi anamulimbikitsa kudalira Mulungu wa Naomi? | Funsani ana ajambule dzanja lawo polemba mzere kuzungulira dzanjalo pa papela. Lembani 'KUKHULUPIRIKA' pakati pa dzanjalo. Pa chala chilichonse ndi chala chachikulu lembani mawu amene aonetse tanthauzo la kukhulupirika kwa munthu wina. Gawanani ena maganizo anu. Rute anaonetsa kukhulupirika kwakukulu kwa Naomi ndiponso kwa Mulungu wa Naomi. Rute ndi Oripa ankayenera kuchita zisankho. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Rute ndi Naomi ali pa ulendo wopita ku Betelehemu. Ndipo Rute anaonetsa chikondi chake pa Naomi, kudzipereka kwake kwa anthu a Naomi ndi chikhulupiriro chake mwa Mulungu wa Naomi. Ndi imfa yokha imene ikanawasiyanitsa. **(Onani Mavesi Oloweza)**<br>2. Munali chisangalalo mu Betelehemu pamene anaona Naomi ndi Rute atabwerera pa nthawi imene ankayamba kukolola barele. ***(1: 19)***<br>3. Nthawi zambiri mayina amakhala ndi matanthauzo; nthawi zina dzina limagwirizana ndi chomwe munthuyo ali, nthawi zina ayi. Naomi kutanthauza kuti 'wosangalatsa' koma tsopano anafuna anthu amutchule kuti Mara kutanthauza 'kuwawidwa'.<br>4. Naomi anali ndi zifukwa zomwe ankafunira kusintha dzina lake; iye anapita 'wolemera' pamodzi ndi mwamuna wake ndi ana ake, koma tsopano akubwera 'wosauka' wopanda aliyense. Mulungu Wamphamvuzonse anamugwetsera mavuto owawa moyo wake. ***(1: 20-21)***<br>5. Rute anafuna kugwira ntchito kuti apeze chakudya chake ndi cha Naomi. Iye anapeza ntchito m'munda mwa Boazi, mlimi wachuma amenenso anali m'bale wa Elimeleki. ***(2: 1-3)***<br>6. *Ganizirani zomwe Mulungu ankachita pa moyo wa Rute pomubweretsa ku Betelehemu ndi kumutsogolera ku munda umene adzakumana ndi Boazi.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kubwerera kwa akazi amasiye. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Kunali kukhetsa misozi pamene Oripa ankatsanzika kubwerera kwa abale ake ndi kwa milungu yawo yabodza. ***(1: 14)***<br>2. Rute analengeza za chikhulupiriro chake mwa Mulungu, za kukhulupirika kwake kwa Naomi ndi chikhumbo chake chokhala naye, kutenga anthu a Naomi kukhala anthu ake, Mulungu wa Naomi kukhala Mulungu wake, kumene Naomi akafere, iyenso akafera komweko. Imfa yokha ndiye idzawasiyanitsa. ***(Mavesi Oloweza)***<br>3. *N'kofunika kukhala okhulupirika kwa abale ndi abwenzi; koma kudzipereka kwa Ambuye Yesu ndiye kofunika kwambiri.*<br>4. Kufika kwa Naomi ndi Rute mu Betelehemu kunatekesa anthu. Inali nthawi yoyamba kukolola barele. Naomi anapempha kuti azimutchula kuti Mara kutanthauza 'kuwawidwa' m'malo mwa Naomi zomwe zinkatanthuza 'wosangalatsa'. Iye anachoka ku Betelehemu 'wolemera' pamodzi ndi mwamuna wake ndi ana ake, koma wabwerera ali 'wosauka'. ***(1: 19-22)***<br>5. *Zinthu zowawa zinathandiza Naomi kuti akaone njira yake yobwerera kwa Mulungu. Iye anavomereza kulakwa kwake kwa kale ndipo Mulungu mwa chifundo chake anamubweretsa kwawo ali bwino.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Naomi abwerera kwa Mulungu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Awiriawiri, mukhala ndi nthawi yofunsa Naomi; aliyense akhale ndi mafunso awiri kapena atatu ofunsa Naomi. | Lembani nkhani yayifupi mu nyuzi ya Betelehemu ndipo mutu wake ukhale 'Mayi Wamasiye Wokhumudwa Abwerera Kwawo'. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Si nthawi zonse pomwe zovuta pa moyo wathu zimabwera chifukwa cha zisankho zoyipa tinachita, koma ngati tichita zisankho zoyipa, tikuyenera kukonzeka kuvomereza kulephera kwathu ndi kupempha chikhululukiro kwa Mulungu (ndiponso mwina kwa amene tinawalakwira).<br>2. Kodi tikukhulupirira Mulungu kuti angathe kutithandiza pamene tikukumana zinthu zatsopano; monga, kusintha malo ophunzirira? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi mukuganiza kuti ndi chifukwa chiyani Naomi anatichitsa Rute kukhala wokhulupirika motero? Kodi ena angafune kukhulupirira Khristu chifukwa cha zimene amaona mwa inu ndi ine?<br>2. Werengani ***Luka 15: 11-24*** kapena ***1 Yohane 1: 9***. Kodi mavesi amenewa akutilimbikitsa motani za kuvomereza pamene tachita cholakwa (tachimwa)?<br>3. Kodi akuphunzitsa chiyani za chikhululukiro cha Mulungu? |

| | C5 – KALASI 3<br>Phunziro Lachitatu – Rute<br>Mutu – M'bale wachuma | C5 – KALASI 4<br>Phunziro Lachitatu – Rute<br>Mutu – Amayi amasiye otsogozedwa ndi Mulungu |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Rute 2: 1-23***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Rute 2: 20***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu ankayang'anira Rute ndi Naomi ndipo anatsogolera Rute ku munda wa Boazi, m'bale wawo, amene anakomera mtima Rute ndi kumuteteza.<br>2. Ngakhale pamene tikukumana ndi mavuto m'moyo wathu tingathe kudalira Mulungu kuti adzatsogolera ku zinthu zabwino kwambiri. | **Werengani:** ***Rute 2: 1-23***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Rute 2: 20***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Nthawi yokolola inapereka mwayi kwa Rute wogwira ntchito kuti apeze chakudya cha Naomi ndi chake.<br>2. Boazi akusamala bwino ndi kumpatsa Rute, mlendo, zosowa zake chifukwa cha kulimbika ntchito ndi kukhulupirika kwake. Ife tikuyenera kugwira ntchito pa muyeso umene umakondweretsa Mulungu. |
| MAWU OYAMBA | Yerekezani kuti muli pa ulendo tsiku loyamba kupita ku ntchito yatsopano m'dziko lachilendo. Kambiranani m'magulu kapena awiriawiri zomwe mungakhale mukuganiza nthawi imeneyo. Kodi ndi zinthu zofunika zitatu ziti zomwe mungamaganizire? | Kambiranani m'magulu: Kodi ntchito ndi yabwino kwa ife, kapena ndi chinthu 'choyipa choyenera'? ***KAPENA***<br>Awiriawiri, mwini ntchito ndi wantchito, kambiranani muyeso wa kagwiridwe ka ntchito kakuyenera kukhala mwa winayo. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Rute anadzipereka kugwira ntchito kuti athandize Naomi ndi iye mwini. Iye anapita ku munda wa Boazi. Okolola ankadula tirigu ndipo atsikana antchito ankabwera pambuyo ndi kumanga tiriguyo m'mitolo. Tirigu amene atsikana sanamutole ankakhala wa anthu osawuka, amayi amasiye ndi ena kuti atole (kapena kukunkha). ***(2: 1-3)***<br>2. Boazi, mwini munda, anaona Rute ndipo anafunsa kuti anali ndani, ndipo woyang'anira anamuwuza za kulimbika kwake pogwira ntchito. ***(2: 5-7)***<br>3. Boazi anaonetsa kukoma mtima kwa Rute. Iye anawuza Rute kuti akhale pamodzi ndi atsikana ake antchito ndipo azimwa madzi akamva ludzu. Iye anawuza antchito aamuna kuti asamukhudze koma amupatse buledi ndi tirigu okazinga pa nthawi ya kudya. ***(2: 8-9)***<br>4. Rute anathedwa nzeru ndi chifundo chimenechi ndipo monga mlendo, sanali woyenera – *chithunzi cha chikondi cha Mulungu ndi chisomo (chikondi chosatiyenera) chake pa ife.* ***(2: 10-13)***<br>5. Boazi anayamikira kukhulupirika kwa Rute kwa Naomi ndi kwa Mulungu amene anayamba kumukhulupirira.<br>6. Naomi anasangalala ndi chipambano cha Rute tsiku limenelo ndi nkhani ya Boazi. ***(2: 17-23)***<br>7. *Mulungu anali ndi chikonzero ndipo ankatsogolera miyoyo yawo.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – M'bale wachuma. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Lamulo la Mulungu linkati tirigu amene okolola asiya osadula m'mbali mwa munda komanso amene wagwa pansi pamene atsikana akumanga mitolo anali wa amayi amasiye ndi osauka monga Rute kuti atole (kukunkha). ***(2: 1-3)***<br>2. 'Zinachitika' (chinali chikonzero cha Mulungu) kuti Rute ankagwira ntchito m'munda mwa Boazi, m'bale wa Elimeleki. Boazi anaona Rute, anafunsa za iye ndipo anawuzidwa ndi woyang'anira za kulimbika kwake pogwira ntchito. ***(2: 5-7)***<br>3. Boazi anaonetsa kukoma mtima kwa Rute. Iye anawuza Rute kuti akhale pamodzi ndi atsikana ake antchito ndipo azimwa madzi akamva ludzu. Iye anawuza antchito aamuna kuti asamukhudze koma amupatse buledi ndi tirigu okazinga pa nthawi ya kudya. ***(2: 8-9)***<br>4. Rute anathedwa nzeru ndi chifundo chimenechi ndipo monga mlendo, sanali woyenera – *chithunzi cha chikondi cha Mulungu ndi chisomo (chikondi chosatiyenera) chake pa ife.* ***(2: 10-13)***<br>5. Monga munthu wopembedza, Boazi anayamikira Rute chifukwa cha kulimbika kwake pogwira ntchito, kukhulupirika kwake kwa Naomi ndi kwa Mulungu 'amene wabwera pansi pa mapiko ake kuti akuteteze'. ***(2: 11-12)***<br>6. Naomi anasangalala atamva za Boazi. **(Vesi Yoloweza)**<br>7. *Rute anapezeka akukunkha m'munda mwa Boazi, m'bale wa Elimeleki. Pa izi, ndi pa nthawi ya kufika kwawo, tikuona Mulungu akukwaniritsa cholinga chake chabwino pa iwo.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Amayi amasiye otsogozedwa ndi Mulungu. |
| KUKUMBUTSANA | Awiriawiri, pangani mafunso asanu ochokera pa nkhani ya phunziro la lero. Magulu awiri ayesane pakufunsana mafunso. | 'Tsiku langa loyamba kugwira ntchito mu Betelehemu': Yerekezani ndinu Rute mukulemba zochitika kumapeto a tsiku limenelo. Kodi ndi maganizo otani amene iye akanalemba? |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kudalira Mulungu sikunachititse Rute kukhala waulesi. Kodi mukuyembekezera Mulungu kukuthandiza polemba mayeso ngati inu simunawerenge?<br>2. Munthu wa dziko lina wabwera m'kalasi mwanu. Kodi mungamuthandize komanso kukhala mnzake monga anachitira Boazi kwa Rute? Kapena inu mutha kumacheza ndi anzanu okha, osamayankhula naye mlendoyo? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Tsiku limodzi, Rute anakunkha pafupifupi makilogalamu khumi a barele – iyi inali ntchito yowawa kwambiri!<br>Werengani ***Akolose 3: 22-24.***<br>Kodi zochita za Rute ndi mavesi awa zingatilimbikitse motani pa kagwiridwe kathu ka ntchito? |

| | C5 – KALASI 3<br>Phunziro Lachinayi – Rute<br>Mutu – Chifuniro cha Mulungu | C5 – KALASI 4<br>Phunziro Lachinayi – Rute<br>Mutu – Boazi ndi Rute adalitsidwa ndi Mulungu |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***Rute 3: 1-18 ndi 4: 1-17***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Salimo 37: 5***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Naomi anafuna kuti Rute akhale ndi tsogolo labwino choncho anamuthandiza kupeza banja komanso kupereka malo a Elemeleki kwa Rute.<br>2. Mulungu anadalitsa Rute ndi Naomi. Atasankha kutsatira Mulungu osati mafano, Rute anakhala mbali imodzi ya chikonzero cha Mulungu pa chipulumutso chathu. | **Werengani:** ***Rute 3: 1-18 ndi 4: 1-17***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Rute 4: 10***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Naomi anafuna kupanga tsogolo la Rute. Iye anaona mwa m'bale wawo Boazi kuthekera kokhala 'wolowa chokolo' - amene adzagula malo ndi kukwatira Rute ndi cholinga chakuti malo asapite kwa anthu ena.<br>2. Rute ndi Naomi anadalitsidwa moposera muyeso. Atasankha kutsatira Mulungu osati mafano, Rute anakhala mbali imodzi ya chikonzero cha Mulungu pa chipulumutso chathu. |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ana kuti alembe 'm'ndandanda wa makolo' awo pa pepala. Onani ngati angathe kutchula mayina awo mpaka pa agogo a agogo awo. | Mu zikhalidwe za anthu, makolo amasankha oti akwatirane ndi ana awo. Awiriawiri kapena m'magulu, kambiranani ubwino ndi kuyipa kochita zimenezi. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Chikonzero cha Naomi chinali choti Rute apite kwa Boazi kukamupempha kuti akhale wolowa chokolo, kutanthauza kuti agule malo a Elemeleki ndi kukwatira Rute. ***(3: 1-2)***<br>2. Anali madzulo pa nthawi yokolola. Akadya ndi kumwa, Boazi ankagona pakati pa milu ya tirigu kufuna kuteteza kwa anthu akuba.<br>3. Naomi anawuza Rute kuti avale zovala zabwino kwambiri ndipo apite kwa Boazi, amene anali atagona pa mbali pa mulu wa tirigu. Rute anamvera, anapita kwa Boazi, ndipo anagona pansi ndi kumadikira. ***(3: 3-7)***<br>4. Boazi atadzidzimuka usiku anapeza kuti Rute anali atagona ku mapazi ake. Rute anapempha kuti amufunditse ndi mkanjo wake ngati chizindikiro choti iye adzakhala wolowa chokolo. ***(3: 8-9)***<br>5. Iye analonjeza kuthandiza Rute, koma panali wina amene ndi m'bale wawo amene ankayenera kukhala woyamba kumupempha. Boazi anatumiza Rute kwawo ndi tirigu wina wa Naomi. ***(3: 10-15)***<br>6. M'mawa wake Boazi anakumana ndi akuluakulu khumi pamodzi ndi munthu woti alowe chokolo pa chipata cha mzindawo. Popeza munthuyo sanafune kukwatira Rute, Boazi anavomera zomukwatira ndi kumugulira malo. ***(4: 1-6)***<br>7. Naomi anasangalala kwambiri mwana atabadwa wotchedwa Obedi amene chidzukulu chake anali Mfumu Davide. ***(4: 16-17)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Chifuniro cha Mulungu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Naomi ankaganizira za tsogolo lawo – kuti apeze 'wolowa chokolo' kuti agule malo awo ndi kukwatira Rute ndi cholinga chakuti malo akhalebe m'banja mwawo. Iye analangiza Rute kuti apite kwa Boazi mwamseri ndi kukamupempha pa kutha pa tsikulo. ***(3: 1-2)***<br>2. Akakolola tirigu, anthu ankadya, kumwa ndi kugona m'mbali mwa milu ya tirigu akuteteza kwa akuba.<br>3. Rute anapita kukasamba, anadzola mafuta onunkhira ndi kuvala zovala zabwino kwambiri monga zovala za mkwatibwi. Iye anapita kwa Boazi amene anagona pambali pa mulu wa tirigu. Rute anafundula mapazi ake monga anamulangizira Naomi ndipo anagona pamenepo kudikirira. ***(3: 3-6)***<br>4. Atamva kuzizira ku mapazi, Boazi anadzidzimuka ndipo anapeza Rute atagona ku mapazi ake. Rute anapempha kuti amufunditse ndi mkanjo wake ngati chizindikiro choti iye adzakhala wolowa chokolo. ***(3: 9)***<br>5. Boazi anali wokonzeka kumuthandiza koma panali wina amene anali m'bale wawo amene ankayenera kukhala woyamba kumupempha. Boazi anatumiza Rute kwawo ndi tirigu wina wa Naomi. ***(3: 10-15)***<br>6. M'mawa wake Boazi anakumana ndi akuluakulu khumi pamodzi ndi munthu woti alowe chokolo pa chipata cha mzindawo. Popeza munthuyo sanafune kukwatira Rute, Boazi ananena kuti amukwatira; anagwirizana posinthana nsapato. ***(4: 1-8)***<br>7. Naomi anasangalala kwambiri mwana atabadwa wotchedwa Obedi amene chidzukulu chake anali Mfumu Davide. ***(4: 16-17)***<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Boazi ndi Rute adalitsidwa ndi Mulungu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Pangani pepala loyika m'buku ndi kulembapo mawu ena a mu **Vesi Yoloweza**. Pamene mukugwira ntchito muziganizira nkhani ya Rute yomwe akufotokoza mu vesi imeneyi. | Awiriawiri kapena magulu ang'onoang'ono, konzekerani mafunso a pa kanema ofunsa Boazi ndi Rute pa za ukwati wawo. Kodi atsikana angamufunse Rute chiyani? Nanga anyamata angafune kufunsa Boazi chiyani? |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>• Patatha zaka 1000, mu Betelehemu momwemo, Mulungu analola kuti Mwana wake abadwe m'banja limene kholo lake anali Boazi ndi Rute. Motero, mtsikana wa Chimoabu amene poyamba ankapembedza mafano, anakhala gawo limodzi la mbiri ya chikonzero cha Mulungu cha chipulumutso chathu.<br>• Kodi chisankho chake chodalira Mulungu chinali chofunika motani?<br>• Pamene takhulupirira Mulungu ndi Ambuye Yesu kukhala Mpulumutsi wathu, kodi ndani angadziwe zotsatira za chisankho chimenechi? Ndi Mulungu yekha amene angadziwe! | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Werengani ***1 Akorinto 6:19-20*** ndi ***1 Petro 1:18-19***.<br>• Kodi Khristu analipira dipo lotani pamene anatiwombola ife, anthu ochimwa, ndi kutilowetsa m'banja la Mulungu?<br>• Ngati tinawomboledwa ndi mtengowapatali umenewo, tikuyenera kulemekeza (kubweretsa ulemerero) Mulungu m'malo momadzikondweretsa tokha.<br>• Kodi izi timachita motani kudzera m'makhalidwe athu ndi mu zisankho zathu zimene timachita tsiku ndi tsiku? |

| | C6 – KALASI 3<br>Phunziro Loyamba – Samueli<br>Mutu – Kupemphera kwa Mulungu | C6 – KALASI 4<br>Phunziro Loyamba – Samueli<br>Mutu – Kupemphera kwa Mulungu |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***1 Samueli 1: 1-28***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 1: 10-11***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Hana anapempha Mulungu mwana wamwamuna.<br>2. Mulungu amamva ndi kuyankha mapemphero athu pamene tili ndi chosowa. | **Werengani:** ***1 Samueli 1: 1-28***<br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 6: 5-8***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Hana anapempha Mulungu mwana wamwamuna.<br>2. Mulungu amamva ndi kuyankha mapemphero athu. |
| MAWU OYAMBA | Lembani zinthu zisanu zofunika zomwe mukuganiza kuti ndi zimene anthu apempha kwa Mulungu. Kenaka kambiranani maganizo anu pa gulu. | Kambiranani zinthu izi, poyamba awiriawiri, kenaka mukhale pamodzi ndi awiri ena kuti mumve maganizo awo:<br>1. N'chifukwa chiyani anthu amapemphera?<br>2. Kodi titha kupemphera mmene tingafunire?<br>3. Kodi anthu ambiri amapempha chiyani kwa Mulungu?<br>4. Kodi anthu amapemphera nthawi zanji? |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Elikana anali ndi akazi awiri – Penina ndi Hana. Penina anali ndi ana koma Hana analibe mwana. ***(1: 1-2)***<br>2. Atafika ku Nyumba ya Yehova, Hana anali ndi chisoni kwambiri chifukwa Penina ankamuzunza. Hana analira ndi kupemphera kwa Mulungu. ***(1: 3-10)***<br>3. Hana analonjeza kwa Mulungu kuti akamupatsa mwana wamwamuna, iye adzamupereka kwa Mulungu. ***(1: 11)***<br>4. Eli, wansembe, anaweruza Hana molakwika pakuti ankaganiza kuti waledzera chifukwa ankaona milomo yake ikugwedera koma sankamva mawu.<br>5. Hana anafotokoza kuti ankatula nkhawa zake kwa Mulungu. Eli anazindikira kuti ankanena zoona ndipo anamudalitsa. ***(1: 12-18)***<br>6. Mulungu anakumbukira Hana ndipo anamupatsa mwana wamwamuna. Hana anamutchula kuti Samueli ndipo kenaka anakwaniritsa lonjezo lake lomupereka kwa Yehova. ***(1: 20)***<br>7. *Fotokozani kuti titha kubweretsa mavuto athu onse kwa Mulungu mu pemphero, koma nthawi zambiri sayankha mmene ife timaganizira.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kupemphera kwa Mulungu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Elikana anali ndi akazi awiri – Penina ndi Hana. Penina anali ndi ana koma Hana analibe mwana. ***(1: 1-2)***<br>2. Atafika ku Nyumba ya Yehova, Hana anali ndi chisoni kwambiri chifukwa Penina ankamuzunza. Hana analira ndi kupemphera kwa Mulungu. ***(1: 3-10)***<br>3. Hana analonjeza kwa Mulungu kuti akamupatsa mwana wamwamuna, iye adzamupereka kwa Mulungu. ***(1: 11)***<br>4. Eli, wansembe, anaweruza Hana molakwika pakuti ankaganiza kuti waledzera chifukwa ankaona milomo yake ikugwedera koma sankamva mawu.<br>5. Hana anafotokoza kuti ankatula nkhawa zake kwa Mulungu. Eli anazindikira kuti ankanena zoona ndipo anamudalitsa. ***(1: 12-18)***<br>6. Mulungu anakumbukira Hana ndipo anamupatsa mwana wamwamuna. Hana anamutchula kuti Samueli ndipo kenaka anakwaniritsa lonjezo lake lomupereka kwa Yehova. ***(1: 20-28)***<br>7. *Fotokozani kuti titha kubweretsa mavuto athu onse kwa Mulungu mu pemphero, koma nthawi zambiri sayankha mmene ife timaganizira.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Loyamba.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kupemphera kwa Mulungu. |
| KUKUMBUTSANA | Jambulani zidole za nkhani iyi, gwiritsani ntchito zithunzi zisanu ndi chimodzi. Gwiritsani ntchito mawu a m'mabokosi pamene n'kofunika kutero. Izi achite awiriawiri kapena pa m'gulu ang'onoang'ono. | Awiriawiri, pezani pepala pamene mulembe zomwe mwaphunzira za pemphero m'phunziro lino. Ganizirani mfundo khumi ndi kuzilemba mutaziganizira mozama. |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Hana anapita kwa Mulungu pamene anali ndi chisoni ndi nkhawa. Kodi ife tingachite zomwezi? Kodi pemphero ndi lofunika motani kwa aliyense wa ife?<br>2. Hana anasunga lonjezo lake lopereka mwana wake kwa Yehova – kodi ife timasunga malonjezo anthu nthawi zonse? Kodi tikuyenera kulonjeza kwa Mulungu? | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kodi ndi liti limene munalonjezapo?<br>2. Kodi munasunga lonjezolo?<br>3. Kodi tikuyenera kulonjeza kwa Mulungu?<br>4. Kuchokera pa **Vesi Yoloweza** pa ***Mateyu 6: 5-8***, kodi tikuphunzira chiyani za pemphero?<br>5. Ganizirani nthawi imene Mulungu anayankha mapemphero anu ndipo mufotokozere gulu. |

| | **C6 – KALASI 3**<br>**Phunziro Lachiwiri – Samueli**<br>**Mutu – Kukula pamaso pa Mulungu** | **C6 – KALASI 4**<br>**Phunziro Lachiwiri – Samueli**<br>**Mutu – Kukula pamaso pa Mulungu** |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***1 Samueli 2: 1-9, 18-21, 26, 34***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 2: 30***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu anadalitsa Hana ndipo iye anayamika chifukwa cha kubadwa kwa Samueli. Mwaufulu wake anapereka Samueli kwa Yehova. Samueli anakula ndipo anapeza chisomo pamaso pa Mulungu.<br>2. Mulungu amalemekeza amene amalemekeza Iye. | **Werengani:** ***1 Samueli 2: 1-36***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 2: 30***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu anadalitsa Hana ndipo iye anayamika chifukwa cha kubadwa kwa Samueli.<br>2. Mwaufulu wake anapereka Samueli kwa Yehova. Samueli anakula ndipo anapeza chisomo pamaso pa Mulungu.<br>3. Mulungu amalemekeza amene amalemekeza Iye. |
| **MAWU OYAMBA** | Kodi ndi liti lomwe inu munatamanda Mulungu? Ganizirani zinthu zosiyanasiyana zomwe tingamuyamike nazo Mulungu komanso njira zosiyanasiyana zomwe tingamutamandire ndi kumulemekeza Iye. | Ganizirani zinthu zosiyanasiyana zomwe tingamuyamike nazo Mulungu komanso njira zosiyanasiyana zomwe tingamutamandire ndi kumulemekeza Iye. |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Hana anasangala chifukwa Mulungu anamupatsa mwana wamwamuna. Iye anayamika Mulungu chifukwa cha zonse zimene Iye ali ndiponso ndi zonse zimene anamuchitira. ***(2: 1-10)*** Iye anali wokondwa chifukwa anasunga mawu ake ndi kupereka Samueli kwa Yehova.<br>2. Samueli anakula akutumikira Mulungu m'Nyumba yake. Chaka chilichonse amayi ake ankabwera kudzamuona ndi kumubweretsera zovala zatsopano. ***(2: 18-19)***<br>3. Eli anapempha Mulungu kuti amupatse Hana ana ena ambiri. Mulungu anadalitsa Hana ndi ana ena asanu. ***(2: 20-21)***<br>4. Samueli anagwira ntchito molimbika ndipo anapeza kuyanja pamaso pa Yehova. ***(2: 26)***<br>5. Ana a Eli anachimwa ndipo Mulungu anawalanga. ***(2: 34)***<br>6. *Ganizirani za kusiyana kwa pakati pa Samueli amene anakondweretsa Mulungu ndi ana a Eli amene sanamvere malamulo a Mulungu ndipo analangidwa.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kukula pamaso pa Mulungu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Hana anasangala chifukwa Mulungu anamupatsa mwana wamwamuna. Iye anayamika Mulungu chifukwa cha zonse zimene Iye ali ndiponso ndi zonse zimene anamuchitira. ***(2: 1-10)*** Iye anali wokondwa chifukwa anasunga mawu ake ndi kupereka Samueli kwa Yehova.<br>2. Samueli anakula akutumikira Mulungu m'Nyumba yake. Chaka chilichonse amayi ake ankabwera kudzamuona ndi kumubweretsera zovala zatsopano. ***(2: 18-19)***<br>3. Eli anapempha Mulungu kuti amupatse Hana ana ena ambiri. Mulungu anadalitsa Hana ndi ana ena asanu. ***(2: 20-21)***<br>4. Samueli anagwira ntchito molimbika ndipo anapeza kuyanja pamaso pa Yehova. ***(2: 26)***<br>5. Ana a Eli anachimwa ndipo Mulungu anawalanga. Iwo sanamvere malamulo amene Mulungu anawapatsa okhudzana ndi ntchito ya unsembe. ***(2: 34)***<br>6. *Ganizirani za kusiyana kwa pakati pa Samueli amene anakondweretsa Mulungu ndi ana a Eli amene sanamvere malamulo a Mulungu ndipo analangidwa.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachiwiri.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kukula pamaso pa Mulungu. |
| **KUKUMBUTSANA** | 1. Ganizirani zisankho zimene mukufuna kudzachita m'tsogolo. Kodi mudzalemekeza Mulungu motani mu zisankhozo? Kambiranani awiriawiri kenaka ndi gulu lonse.<br>2. Jambulani chithunzi chomwe chidzaonetsa njira zimene Mulungu adzalemekezedwa nazo m'moyo wanu. | 1. Werengani ***Salimo 103: 1-5***. Lembani pemphero, kutamanda Mulungu chifukwa cha zinthu zabwino wachita pa moyo wanu.<br>2. Fufuzani za moyo wa Eric Liddel. Kodi iye analemekeza Mulungu motani?<br>3. Kambiranani momwe tingalemekezere Mulungu pa ntchito iliyonse watipatsa. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Onaninso pa ***Akolose 3: 23***. Kodi tikhale ndi maganizo otani pa kagwiridwe ka ntchito kathu?<br>2. Kodi mumalemekeza Mulungu pa zonse zimene mumachita?<br>3. Pempherani kuti Mulungu akuthandizeni kumulemekeza mu zisankho zanu. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Pempherani kuti Mulungu akuthandizeni kumulemekeza pa moyo wanu wa tsiku ndi tsiku.<br>2. Kambiranani makhalidwe a kagwiridwe ka ntchito ka Mkhristu. Onaninso pa ***Akolose 3: 23***. |

| | C6 – KALASI 3<br>Phunziro Lachitatu – Samueli<br>Mutu – Kumvetsera kwa Mulungu | C6 – KALASI 4<br>Phunziro Lachitatu – Samueli<br>Mutu – Kumvetsera kwa Mulungu |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***1 Samueli 3: 1-21***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 3: 10***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu anayamba kuyankhula kwa Samueli.<br>2. Mulungu akuyankhulabe ndi anthu lero kudzera m'Baibulo. | **Werengani:** ***1 Samueli 3: 1-21***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 3: 10***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu anayamba kuyankhula kwa Samueli.<br>2. Mulungu akuyankhulabe kudzera m'Baibulo kwa amene amamvetsera kwa Iye. |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ana, "Kodi iwo amatha kumvetsera bwino?"<br>Awerengereni mosafulumira ndime ya mawu makumi awiri pa mutu wina uliwonse (monga, chakudya, nyama ndi zina zambiri). Mwadala musiye mawu amene akuyembekezera kuti awamva pa mutu umenewo. Mukatsiriza, apatseni mphindi ziwiri kuti alembe mawu onse amene angathe kuwakumbukira. Onani ngati wina walemba mawu amene inu simunayankhule.<br>Onani amene wapereka mayankho ambiri olondola. | Funsani ana aganize za munthu amene akumudziwa kuti amadziwa kumvetsera bwino.<br>N'chifukwa chiyani asankha munthu ameneyo?<br>Kodi iwo angadziwe bwanji kuti munthuyo akumvetsera?<br>Funsani, "Kodi ndinu omvetsera abwino?" |
| **KUTSIRIZA** | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Samueli anali mnyamata wamng'ono amene sankadziwa Mulungu pamene nkhani ya mu chaputala ichi inachitika.<br>2. Usiku wina, Samueli atagona pa malo pake, anamva mawu akuyitana dzina lake. ***(3: 1-4)***<br>3. Poganiza kuti anali Eli, Samueli anadzuka ndi kuthamanga kuti akamve chimene akufuna. Eli anati iye sanamuyitane. ***(3: 5-6)***<br>4. Izi zinachitika katatu Eli asanazindikire kuti anali Yehova amene ankayitana Samueli, choncho anamuwuza Samueli zoti akuyankhule akamuyitananso. ***(3: 8-9)***<br>5. Mulungu anayitananso Samueli ndipo nthawi iyi Samueli anayankha monga anamuwuzira Eli. ***(3: 10)***<br>6. Mulungu anamupatsa Samueli uthenga wa zimene zidzachitika posachedwa m'banja la Eli. ***(3: 11-14)***<br>7. Mmawa Samueli anawuza Eli uthengawo. Iye ankachita mantha koma Eli anamuwuza kuti asabise china chilichonse. ***(3: 15-18)***<br>8. Mu zaka zambiri zam'tsogolo, Mulungu anapitiriza kuyankhula ndi Samueli, ndipo anthu anazindikira kuti anali mneneri wa Mulungu. **(3: 19-21)**<br>9. *Fotokozani kuti nthawi imeneyo, Baibulo kunalibe, ndipo Mulungu ankayankhula kwa anthu yekha kudzera mwa anthu amene ankawasankha. Nthawi zina anthuwa ankatchedwa aneneri ndipo ntchito yawo inali kuwuza anthu ena uthenga umene amva.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kumvetsera kwa Mulungu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Samueli anali mnyamata wamng'ono amene sankadziwa Mulungu pamene nkhani ya mu chaputala ichi inakachitika.<br>2. Usiku wina, Samueli atagona pa malo pake, anamva mawu akuyitana dzina lake. ***(3: 1-4)***<br>3. Poganiza kuti anali Eli, Samueli anadzuka ndi kuthamanga kuti akamve chimene akufuna. Eli anati iye sanamuyitane. ***(3: 5)***<br>4. Izi zinachitika katatu Eli asanazindikire kuti anali Yehova amene ankayitana Samueli, choncho anamuwuza Samueli zoti akuyankhule akamuyitananso. ***(3: 8-9)***<br>5. Mulungu anayitananso Samueli ndipo nthawi iyi Samueli anayankha monga anamuwuzira Eli. ***(3: 10)***<br>6. Mulungu anamupatsa Samueli uthenga wa zimene zidzachitika posachedwa m'banja la Eli. ***(3: 11-14)***<br>7. Mmawa Samueli anawuza Eli uthengawo. Iye ankachita mantha koma Eli anamuwuza kuti asabise china chilichonse. ***(3: 15-18)***<br>8. Mu zaka zambiri zam'tsogolo, Mulungu anapitiriza kuyankhula ndi Samueli, ndipo anthu anazindikira kuti anali mneneri wa Mulungu. ***(3: 19-21)***<br>9. *Fotokozani kuti nthawi imeneyo, Baibulo kunalibe, ndipo Mulungu ankayankhula kwa anthu yekha kudzera mwa anthu amene ankawasankha. Nthawi zina anthuwa ankatchedwa aneneri ndipo ntchito yawo inali kuwuza anthu ena uthenga umene amva.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachitatu.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kumvetsera kwa Mulungu. |
| **KUKUMBUTSANA** | Werengani ***2 Timoteo 3: 16***.<br>Kambiranani njira zimene Mulungu atha kuyankhula kwa ife kuchokera m'Baibulo pamene tikuwerenga tsiku lililonse.<br>Ndi zofunika kuti Akhristu aziwerenga Baibulo nthawi zonse. Kambiranani njira zomwe zingathandize kumachita zimenezi. | Werengani ***Yobu 33: 14-18*** ndi ***Luka 6: 46-49***. Kambiranani chifukwa chomwe ndi njira zomwe Mulungu amayankhulira ndi anthu lero.<br>Fotokozani kufunika kwa Baibulo.<br>N'chifukwa chiyani kuli kofunika kuti Akhristu aziwerenga Baibulo nthawi zonse? Awiriawiri, pezani njira zomwe zingathandize kumachita zimenezi. |
| **KHALANI MOYO UMENEWU** | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Kambiranani kutalika kwa nthawi imene mumakhala mukupemphera ndi kuwerenga Baibulo – Kodi ndi yokwanira? Kodi mutha kuchita kuposa pamenepo?<br>2. Ngati simukudziwa kuti mungayambe bwanji kuwerenga Baibulo nokha, funsani mtsogoleri akuthandizeni. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Dzifunseni ngati muli ndi nthawi yokwanira yomvetsera kwa Mulungu ndi kumva zimene Iye akunena kwa inu.<br>2. Pezani njira yoti mutalikitse nthawi yomwe mumapemphera ndi kuwerenga Baibulo. |

| | C6 – KALASI 3<br>Phunziro Lachinayi – Samueli<br>Mutu – Kugwira ntchito ya Mulungu | C6 – KALASI 4<br>Phunziro Lachinayi – Samueli<br>Mutu – Kugwira ntchito ya Mulungu |
|---|---|---|
| | **Werengani:** ***1 Samueli 8: 1-9; 9: 1-8, 14-27; 10: 1***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 9: 6***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu analamula Samueli kuti adzodze mfumu ya Israyeli. Samueli anatenga gawo lofunika kwambiri mu mbiri chifukwa cha ubale wake ndi Mulungu.<br>2. Miyoyo yathu imakhala ndi cholinga pamene tikutsatira Mulungu kwathunthu. | **Werengani:** ***1 Samuel 8: 1-10; 9: 1-27; 10: 1***<br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Samuel 9: 6***<br><br>**Ife tikuphunzira kuti:**<br>1. Mulungu analamula Samueli kuti adzodze mfumu ya Israyeli.<br>2. Mulungu amalamulira zochitika kuti zikwaniritse zolinga zake. Miyoyo yathu imakhala ndi cholinga pamene tikutsatira Mulungu kwathunthu. |
| MAWU OYAMBA | Chitani sewero lalifupi la 'Tsatira Mtsogoleri'. Sankhani mwana kuti akhale 'mtsogoleri'. Kenaka iye atsogolere anzake kuzungulira m'chipindamo, akuchita zizindikiro ndi phokoso zomwe iye akuyenera kumatsanzira. Chitani kawiri koma mofulumira seweroli, nthawi iliyonse ndi mtsogoleri wina.<br><br>Ana akhalenso pansi pa malo awo ndipo afunseni alembe zomwe akuganiza kuti ndi makhalidwe amene mtsogoleri wabwino akuyenera kukhala nawo. Lembani nambala kuyamba ndi khalidwe lofunika kwambiri kenaka kambiranani maganizo amenewo pa gulu. M'njira ina, izi atha kuchita awiriawiri. | Awiriawiri, lembani makhalidwe asanu a mtsogoleri wabwino, kenaka lembani makhalidwe asanu a mtsogoleri woyipa.<br><br>Fananitsani mayankho anu pa gulu ndi kukambirana. |
| KUTSIRIZA | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Zachisoni, ana aamuna a Samueli sanali osiyana ndi ana a Eli pakuti sanali atsogoleri abwino ndipo sankatha kulowa m'malo mwa Samueli amene tsopano anali atakalamba. ***(8: 1-3)***<br>2. Anthu a Israyeli anapempha Samueli kuti asankhe mfumu kuti iziwalamulira, koma Samueli sanakondwere nazo. ***(8: 6)***<br>3. Nayenso Mulungu sanakondwere nazo chifukwa anthu anakana kuti Iye akhale mfumu yawo yokha. ***(8: 6-9)***<br>4. Mulungu anawuza Samueli kuti achenjeze anthu zomwe mfumu idzachita ikadzayamba kulamulira. ***(8: 10-18)*** Koma anthu anakana kumvera.<br>5. Sauli, wa fuko la Benjamini, ananyamuka kukafuna abulu a abambo ake amene anasowa. Iye anayenda mtunda wautali koma sanawapeze. ***(9: 1-5)***<br>6. Wantchito wa Sauli anapereka maganizo akuti iwo apite kwa Samueli kuti akapeze thandizo chifukwa anali mneneri wolemekezedwa wa Mulungu. ***(9: 6)***<br>7. Mulungu anatsogolera Sauli kuti akakumane ndi Samueli ndi kumuwuza kuti uyu ndiye munthu amene wasankha kuti akhale mfumu. Samueli anadya ndi Sauli ndipo kenaka anamudzoza kuti akhale mfumu. ***(9: 14-27; 10: 1)***<br>8. *Samueli anali mneneri wamkulu ndi woweruza. Chinsinsi cha ukulu wake chinali ubale wake wabwino kwambiri ndi Mulungu. Miyoyo itha kukhala yofunika ngati tilola Mulungu kuti ayilamulire kwathunthu.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kugwira ntchito ya Mulungu. | **Perekani Nkhani ya m'Baibulo**<br><br>**Kambiranani ndi Kufotokoza:**<br>1. Zachisoni, ana aamuna a Samueli sanali osiyana ndi ana a Eli pakuti sanali atsogoleri abwino ndipo sankatha kulowa m'malo mwa Samueli amene tsopano anali atakalamba. ***(8: 1-3)***<br>2. Anthu a Israyeli anapempha Samueli kuti asankhe mfumu kuti iziwalamulira, koma Samueli sanakondwere nazo. ***(8: 6)***<br>3. Nayenso Mulungu sanakondwere nazo chifukwa anthu anakana kuti Iye akhale mfumu yawo yokha. ***(8: 6-9)***<br>4. Iye anawuza Samueli kuti achenjeze anthu zomwe mfumu idzachita ikadzayamba kulamulira. ***(8: 10-18)*** Koma anthu anakana kumvera.<br>5. Sauli, wa fuko la Benjamini, ananyamuka kukafuna abulu a abambo ake amene anasowa. Iye anayenda mtunda wautali koma sanawapeze. ***(9: 1-5)***<br>6. Wantchito wa Sauli anapereka maganizo akuti iwo apite kwa Samueli kuti akapeze thandizo chifukwa anali mneneri wolemekezedwa wa Mulungu. ***(9: 6)***<br>7. Mulungu anatsogolera Sauli kuti akakumane ndi Samueli ndi kumuwuza kuti uyu ndiye munthu amene wasankha kuti akhale mfumu. Samueli anadya ndi Sauli ndipo kenaka anamudzoza kuti akhale mfumu. ***(9: 14-27; 10: 1)***<br>8. *Samueli anali mneneri wamkulu ndi woweruza. Chinsinsi cha ukulu wake chinali ubale wake wabwino kwambiri ndi Mulungu. Miyoyo itha kukhala yofunika khala ngati tilola Mulungu kuti ayilamulire kwathunthu.*<br><br>**Fotokozani Vesi Yoloweza ndipo limbikitsani ophunzira kuti aloweze.**<br>**Tsirizani Phunziro Lachinayi.**<br><br>**Kuonetsa:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Kugwira ntchito ya Mulungu. |
| KUKUMBUTSANA | Kambiranani: Kodi mwaphunzira chiyani mu phunziro lino za kukhazikitsa ubale ndi Mulungu?<br>Ganizirani makhalidwe amene Samueli anali nawo omwe mumawasirira. Konzani posita kuti mulembepo zimenezi, kugwiritsa ntchito mawu kapena zithunzi kapena zonse pamodzi. | Werengani ***Salimo 15.*** Kodi Mulungu amafuna kuti ife tikhale anthu otani?<br>Lembani mzere pakati pa pepala kuti mupange mbali ziwiri. Mbali imodzi, lembani zinthu zonse zimene Salimo likunena kuti tizichita; mbali inayo lembani zimene Salimo likuti tisamachite. |
| KHALANI MOYO UMENEWU | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>Funsani Mulungu kuti akuthandizeni kukhazikitsa ubale ndi Iye kuti akwaniritse zolinga zake m'moyo wanu monga anachitira ndi Samueli. | **Zomwe tikuphunzira m'phunziroli:**<br>1. Yamikani Mulungu chifukwa angathe kutsogolera zochitika m'miyoyo yathu kuti akwaniritse zolinga zake monga anachitira ndi Samueli.<br>2. Pemphani Mulungu kuti akuthandizeni kukhala munthu amene Iye akufuna kuti akwaniritse zolinga zake m'moyo wanu. |

# Malangizo a Aphunzitsi a Kachongedwe ka Maphunziro

**Maphunziro a Kalasi Lachitatu**
- Ophunzira sangatsirize maphunziro awa popanda kuwerenga Baibulo ndipo akuyenera kuwerenga ndime imodzi kapena zambiri.
- Kafunsidwe n'kosiyanasiyana, pena pali mabokosi, pena pali mawu amene akusowa ndi njira zina zambiri.
- Mafunso akonzedwa kuti aziyankhidwa kuchokera m'baibulo la Mawu a Mulungu mu Chichewa Chalero ndi Buku Lopatulika ndi Mawu a Mulungu.
- Cholinga chathu n'chakuti ophunzira onse, kaya akugwiritsa Baibulo la mtundu wanji, azitha kuyankha mafunso.
- Sabata lililonse lili ndi marikisi 20 ndipo pa mwezi pali marikisi 80, ngati munthu wakhonza bwino maphunziro onse.
- Kalasi Lachitatu - Pali marikisi imodzi pa yankho, monga momwe tasonyezera.

**Maphunziro a Kalasi Lachinayi**
- Awa ndi maphunziro ovutirapo kusiyana ndi Maphunziro a Kalasi Lachitatu.
- Muli mafunso ovutirapo ofuna mayankho.
- Marikisi 20 pa sabata ndi marikisi makumi 80 pa mwezi ngati amaliza maphunziro molondola ndiponso mafunso onse ali ndi mayankho ake.

**FUNDO ZA KACHONGEDWE**
Choyamba aphunzitsi akupemphedwa kuti:
- Onani phunziro lililonse ndipo chongani moyenera zolondola kapena zolakwitsa.
- Perekani marikisi amene mwalangizidwa kutero.
- Nthawi zonse chongani pogwiritsa ntchito mitundu yosiyana ya zolembera, CHONGANI yankho lolondola.
- Lembani yankho lolondola poyenera kutero ndi kukonza mawu olakwika kalembedwe ake, koma MUSACHOTSE marikisi.
- Perekani marikisi ochepa pa yankho lolondola mbali imodzi yokha.
- Phatikizani marikisi onse a pa mwezi ndipo lembani kumapeto pa malo amene mwapatsidwa.

N'kofunika kusaumira ndi kuchita chilichonse chothandiza kulimbikitsa ophunzira kuti aphunzire Baibulo lawo. N'zothandizanso kuti kumapeto kwa mwezi uliwonse mphunzitsi azilemba mawu a chilimbikitso kwa wophunzira pa malo amene aperekedwa. Mutha kulemba ndemanga yoyamikira kuchekenira bwino, zilembo zabwino ndi kumvetsa bwino phunziro ndi zina zambiri.
Yesetsani kuti ndemanga, mafunso, ziganizo, zomwe mwaona ndi zina zambiri zikhale zosiyanasiyana, kuti zithandize kupanga zinthu kukhala zosiyana. Izi zimafunika kuganiza bwino, ndipo ndi kofunika kuti wophunzira azikhala ndi chidwi nthawi zonse. Ngati chiganizo chomwecho kapena funso lomwe likubwera mwezi uliwonse, zimachotsa chidwi cha wophunzira.

**KALASI Lachitatu**
**Ndemanga zina**
"Ntchito yabwino kwambiri! Inu munamvetsa bwino mafunso onse. Ine ndasangalala ndi yankho la funso lotsiriza limene mwaliyankha bwino kwambiri."
"Moni, Yonatani. Ndikuyamika chifukwa cha kulimbikira kwako. Ndi zosangalatsa kwambiri kuti wayesetsa kuyankha mafunso onse. Ine ndalemba mayankho a mafunso ena amene sunayankhe."

**Ndemanga zauzimu**
"Mose anali ndi mavuto ndi ana a Israyeli, koma Mulungu sanamusiye yekha kuti athetse mavutowo."
"Yosefe sanayiwale kuti abambo ake anamuphunzitsa kukonda Mulungu. Iye anakumbukira zimenezi ngakhale anali kutali ndi kwawo."
"Bartimeyu anatsimikiza mtima zofuna kulandira kuchokera kwa Ambuye Yesu. Iye sanakhumudwitsidwe chifukwa tsopano ankatha kuona ndipo anadziwa kuti Ambuye Yesu anali munthu wapadera kwambiri."

**KALASI Lachinayi**
**Ndemanga zina**
"Maphunziro enanso abwino kwambiri. Zikuoneka kuti tsopano ukumvetsa bwino Nkhani za m'Baibulo ndipo ndikukhulupirira kuti wasangalala nazo. Zikomo kwambiri chifukwa chokhala ndi nthawi yokwanira yochita mosamala maphunzirowa. Zikanatheka kuchita mofulumira, choncho ine ndi kuyamika kwambiri."
"Rakele, wayetsetsa ndithu. Ine ndikaona mayankho akowa, zikuonetsa kuti sunamvetse bwino Nkhani za m'Baibulo. Bwanji uwerengenso zimenezi."

**Ndemanga zauzimu**
"Mafanizo nthawi zina amatchedwa nkhani wamba koma zokhala ndi matanthauzo akumwamba kapena ozama. Kodi ungaganizire tanthauzo lozama la fanizo lomwe lili mu Phunziro 3?"
"Stefano anafa imfa yowawa kwambiri, koma iye sanachite mantha ndi imfa, chifukwa ankadziwa kuti anali ndi Mulungu, ndipo ankadziwa kuti akakhala ndi Ambuye Yesu Kumwamba."

| Zoonjezera A – KALASI Lachitatu Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | **Mutu** | **Nkhani m'Chithunzi** |
| **C1** | **Danieli** | **Dziko lachilendo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/daniel-food/ |
| | | **Ng'anjo yamoto** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/meshach-shadrach-abednego/ |
| | | **Dzanja lodabwitsa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/daniel-feast/ |
| | | **Dzenje la mikango** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/daniel-lions/ |
| | | |
| **C2** | **Anthu Amene Yesu** | **Yesu akumana ndi munthu ku Yeriko** |
| | **Anakumana Nawo** | https://www.freebibleimages.org/illustrations/lgr-zacchaeus/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-077-zacchaeus/ |
| | | **Yesu akumana ndi amayi pa chitsime** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-samaritan-woman/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-018-samaritan-woman/ |
| | | **Yesu akumana ndi munthu usiku** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-017-nicodemus/ |
| | | **Yesu akumana ndi munthu wosaona** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-blind-man/ |

| Zoonjezera A – KALASI Lachinayi Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | **Mutu** | **Nkhani m'Chithunzi** |
| **C1** | **Danieli** | **Kutumikira Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/daniel-food/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/daniel-dream/ |
| | | **Kukhala mbali ya Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/meshach-shadrach-abednego/ |
| | | **Kuyankhulira Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/daniel-feast/ |
| | | **Kuvutika chifukwa cha Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/daniel-lions/ |
| | | |
| **C2** | **Zoyankhula za Yesu** | **Za tchimo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/zacchaeus/ |
| | | **Za kuona** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/blind-man/ |
| | | **Za abusa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-063-good-shepherd/ |
| | | **Za chipulumutso** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-017-nicodemus/ |

| Zoonjezera B – KALASI Lachitatu Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | **Mutu** | **Nkhani m'Chithunzi** |
| **C3** | **Zodabwitsa Zina Zambiri** | **Yesu athandiza munthu wodwala** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-jesus-bethesda/ |
| | | **Yesu athandiza munthu wachisoni** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jairus-daughter/ |
| | | **Yesu athandiza wantchito wa msilikali** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-jesus-centurion/ |
| | | **Yesu athandiza anthu anjala** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-feeding-5000/ |
| | | |
| **C4** | **Imfa ya Khristu** | **Mpsopsono wa womupereka** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-089-prayer-garden/ |
| | | **Chisankho cha bwanamkubwa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-093-mocking-jesus/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-094-pilate/ |
| | | **Manda a munthu wachuma** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-099-jesus-burial/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-101-jesus-resurrection/ |
| | | **Mawu a mlendo** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-103-appearance-emmaus/ |

| Zoonjezera B – KALASI Lachinayi Zithunzi Zaulere m'Baibulo | | |
|---|---|---|
| | **Mutu** | **Nkhani m'Chithunzi** |
| **C3** | **Mphamvu ya Ambuye** | **Kuchiritsa wodwala** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-bethesda/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-029-lame-man/ |
| | | **Kuukitsa akufa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-045-two-miracles/ |
| | | **Kuthandiza osowa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-centurion/ |
| | | **Kudyetsa anthu anjala** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/feeding-5000/ |
| | | |
| **C4** | **Imfa ya Khristu** | **Kuweruzidwa ndi kupachikidwa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-trials/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-crucified-dies/ |
| | | **Kuyikidwa m'manda ndi kuuka!** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/gnpi-099-jesus-burial/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jesus-resurrection/ |
| | | **Kumuona ndi kumva** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/disciples-emmaus/ |
| | | **Kukayikira ndi kukhulupirira** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/resurrection-appearances/ |

## Zoonjezera C – KALASI Lachitatu Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| C5 | Rute | **Zisankho zolakwika** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-1/ |
| | | **Kubwerera kwa akazi amasiye** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-1/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-2/ |
| | | **M'bale wachuma** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-2/ |
| | | **Chifuniro cha Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-3/ |
| | | |
| C6 | Samueli | **Kupemphera kwa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-samuel-saul/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/samuel-born/ |
| | | **Kukula pamaso pa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/samuel-listens/ |
| | | **Kumvetsera kwa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/samuel-listens/ |
| | | **Kugwira ntchito ya Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/samuel-saul/ |

## Zoonjezera C – KALASI Lachinayi Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| C5 | Rute | **Banja lochoka pamaso pa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-1/ |
| | | **Naomi abwerera kwa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-1/ |
| | | **Amayi amasiye otsogozedwa ndi Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-2/ |
| | | **Boazi ndi Rute adalitsidwa ndi Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ruth-3/ |
| | | |
| C6 | Samueli | **Kupemphera kwa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/samuel-born/ |
| | | **Kukula pamaso pa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/samuel-listens/ |
| | | **Kumvetsera kwa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/samuel-listens/ |
| | | **Kugwira ntchito ya Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/samuel-saul/ |

© Bible Educational Services 2020

www.besweb.com

Registered Charity UK CIO 1186004

NY - 12/2024
(Chichewa)